KUKHALA NJIRA YA MULUNGU

MAPHUNZIRO A AKHRISTU ATSOPANO.

WOLEMBA: ARTHUR WALLIS

ZAMKATIMU

Chiyambi

A. A. Dongosolo la maphunziro.
B. B. Zoyenera kwa wophunzira
C. C. Zofunika kwa wophunzitsa.

GAWO 1: KUBWERA MWA KHRISTU

Phunziro 1: Kusintha kwakulu
2: kusankhidwa
3: Zomwe Mulungu wachita
4: Zimene inu mwachita
5: Ubatizo wa madzi
6: Ubatizo wa mzimu

GAWO 2: KUYENDERA LIMODZI

Phunziro 7: Kuzipereka
8: Kukhala mulingo wofunika
9: Chakudya cha pangano
10: Atsogoleri anu
11: Kutengapo mbali
12: Nkhani za chuma
13: Ufumu uli mkudza

GAWO 3: KUKULA MWA MULUNGU

Phunziro 14: Mtima wangwiro
15: Chisomo chodabwitsa
16: Kulankhula ndi ,Mulungu
17: Kugwiritsa ntchito Baibulo
18: Kulimbana ndi mayesero
19: Baibulo ndi chikhalidwe
20: Mawu otsiriza.

CHIYAMBI

DONGOSOLO LA MAPHUNZIRO.

Maphunzirowa akonzedwa kuphunzitsa akhristu atsopano, osati atsogoleri ophunzitsa m'matchalitchi: koma wokhulupirira wozama mchikhulupiriro.

Maphunzirowa atha kuphunzira anthu amene ali mmabanja kapena ena amene sanakwatire. Ndikwabwino ndi koyenera kuti wophunzira wa mkazi aphunzitsidwe ndi mphunzitsi wa mkazi, komanso wa mwamuna aphunzitsidwenso ndi mphunzits wamwamuna. Muyetsetse kuika mfundo zosabvuta pamodzi kuti anyamata atha kuphunzitsana okha okha. Komanso makolo angathenso kuphunzitsa ana awo amene afika pa usinkhu wophunzira.

Mwina mutha kuzifunsa kuti zingatheke bwanji kuti munthu amene Sali mtsogoleri kuphunzitsa wina. Buku la Ahebri linalembedwa kwa okhulupirira aliyense osati kwa atsogoleri a tchalitchi. Wolemba akudzudzula atsogoleriwa chifukwa cha chidodo pophunzira, "ngakhale mwakhala aphunzitsi chifukwa cha nyengoyi, koma ndinu woyenera kuphunzira mawu a Mulungu.(Ahebri 5:11-12)

Mchachidziwikire kuchokera ku chipangano chatsopano kuti wokhulupirira onse ayembekezere kuphunzitsana kapenanso kudzudzulana wina ndi mzake. (Akolose 3:16)

Za chisoni matchalitchi athu adzadza ndi okhulupirira monga akhristu achihebri amene tangotchulidwa atsogoleri koma ndi wofuna kuphunzitsidwanso maziko a chikhulupiriro osati otha kuphunzitsa ena ayi. Itsimikiza kuti "wophunzitsa" apeza phindu mmaphunzirowa kuposa amene ali kuphunzira.

Tafika pa tsiku la uthenga wabwino ndi nthawi yakukolola. Tikuyembekedzera kusanulidwa kwa mzimu woyera kumene kudzangitsa ntchito yopambanayi kuyenda bwino. Nanga matchalitchi ali wokonzeka? Akonzeka kutembenuza wochepa mmalo motembenuza unyinji kwa Ambuye.

Chingathe kukhala chosakondweretsa kuti pamene taika mtima pogwira ntchito koma phindu losaoneka chifukwa chosasamalira. Apa sitiyenera kuloza chala wina koma bvuto ndife eni. Chinthu chofunika ndi chakuti aliyense aphunzitsidwe. Udindo woika okhulupirira kuti aphunzitse ena zimatsatira mlingo wa uzimu wa munthu. Ndikhulupirira kuti akhristu ochuluka, amasokonezeka ndi mabvuto osiyanasiyana amene amkumana nawo, mmalo mozipereka ku ntchito yophunzitsa ana ochepa mchikhulupiriro.(Aroma 2:20)

Chiphunzitso chilli ndi zobvuta zake koma zikhoza kuthetsedwa pokhazikitsa dongosolo la bwino ndi kuunikira kwa akulu a mpingo. Tinenepo zambiri bwino lino. Posafuna

kuwerengera ubwino wa magulu a angóno, kuphunzira pa gulu ndi kwabwinonso polekana ndi njira yophunzitsa mmodzi mmodzi.

1. Pamene munthu wotembenuka amayamba maphunziro, osadikira kuti papezeke ochuluka kaye.
2. Chiphunzitso chimayenda monga mmene wophunzira angathere komanso masiku ena atha kusinthidwa malingana ndi bvuto lomwe lapezeka monga kudwala kapena masiku opuma.
3. Mgwirizano wabwino umabwera pakati pa wophunzira ndi wophunzitsa. Wophunzira amakhala womasuka akakhala ndi zobvuta zina.
4. Wophunzira angathe kupemphera momasuka pa awiri kusiyana ndi pa gulu.

Maphunzirowa amafuna kuti wophunzira azitengapo mbali. Chofunika kwambiri masiku oyambirira a chikhristu ndi "kukhala njira ya Mulungu "pamenenso ndi koyamba kukhala mgulu la akhristu lomwenso ndi gulu la chilendo. Ngakhale mmaphunziri muli uthenga wa mbuku lopatulika, koma ndi zofunika kwambiri kukhala ochitachita osati kudalira kuwerenga kokha.

Palinso ntchito yokachita kunyumba pa mutu umene waphunzitsidwa. Funso lizifunsidwa ndipo mawu owerengedwa aziperekedwa ndi cholinga choti akhazikike. Zikhoza kutheka munthu kukhoza zonse koma moyo wa uzimu osapindula? Inde ngati maphunzirowa sakuwagwiritsa ntchito ku moyo wake. Ndiponso ndikofunikira kuti zomwe ukuchita zizigwirizana ndi zomwe Mulungu akufuna pa moyo wako.

Pamene mphunzitsi ndi wophunzira akumananso mohunziro lina, ayenera kubwereza phunziro limene adphunzira kale pamodzi. Ichi chithandiza kuzamitsa choonadi komanso kukula kwa chikhristu mmiyoyo yawo.

B. ZOFUNIKA KWA WOPHUNZIRA.

Ndikukulandirani ku maphunzirowa ngati inu mkhristu watsopano. Ndili wosangalala podziwa kuti muli mbanja la Mulungu ndipo ndikutengani monga mbale kapena mlongo mwa Khristu.

Ndikhulupirira kuti maphunzirowa akhala mdalitso wopambana kwa inu.
Maphunziro makumi awiri akhala ovitirapo koma mutenge maphunziro pa mulingo umene mungathe kumvetsetsa bwino, ndipo onetsetsani kuti mwakambirana ndi mphunzitsi wanu.

Pali fanizo lina ananena Ambuye wathu Yesu za omanga awiri. Wochenjera anamanga nyumba yake pa thanthwe ndipo mphepo inadza niomba koma nyumbayo siinagwa. Wopusa anamanga nyumba yake pa mchenga ndipo pamene mphepo inaomba pa nyumbayo inagwa ndipo kugwa kwake kunali kwakukulu.
Tiyeni tifanizire izi ndi moyo wathu monga mmene Yesu anachita ndi anthu amene anali kunvera zimene Yesu ananena. Maphunzirowa akuthandizani kuphunzira zimene

Khristu afuna pa moyo wanu monga wophunzira wake. Ndipo zikuthandizani ndi kukulimbikitsani kuti mumvere. Wonani kuti awa ndi maziko a moyo wanu wa chikhristu.

Ambiri amapereka miyoyo yawo kwa Khristu, koma sakhazikika ndi kuteteza chikhulupiriro chawo. Ena amapereka miyoyo yawo pamene ayetsedwa. Amalakwitsa pofuna kukhazikitsa moyo wawo pa maziko a khristu. Amataya nthawi pa zinthu zopanda pake popeza samazindikira kuti ali kumanga nyumba yawo pa mchenga. Ngati mufuna kumanga nyumba yolimba, mangani maziko anu pa Yesu. Munthu wochenjera anali wokondwa pakati pa usiku pamene amanva kuomba kwa mphepo komanso kukukuma kwa madzi chifukwa anakhazikitsa maziko olimba ndiye Khristu.

Ngati uthenga uwu wa Yesu uli chinthu chatsopano kwa inu, mphunzitsi wanu akhala thandizo loposa kuti mumvetse choona m'maphunzirowa ndi kuti mupeze njira yanu mbuku lopatulika. Pamene mukumana ndi zobvuta zina, musatayike poti tiyenera kukumana ndi nkhondo zoterozo kuti tikhoze kuthandizana wina ndi mzake. Pasanapite nthawi inu muzatha kuphunzitsa akhristu atsopano monga mmene inu mwaphunzitsidwira. Kodi ichi sichosangalatsa? Chomwe inu mungafune mmaphunzirowa ndi kukhala ndi buku lanulanu, baibulo lanu la chichewa chomveka bwino ndi kope lolembamo ntchito yokachitra kunyumba.

Maphunzirowa agawidwa magawo atatu. Gawo lililonse lili ndi chiyambi chofotokozera ntchito yonse mmene muchitire mu gawolo. Werengani mutu umene muphunzire musanakumane ndi wokuphunzitsani.Mukayamba mwawerengeratu ndime imene muphunzire, zimathandiza kudziwa zimene zili mu phunzirilo.

Chinthu chofunika koposa mmaphunzirowa ndi kukuphunzitsani inu kulankhula ndi Mulungu pa nokha pa zinthu zimene Mulungu akunena ndi inu pamene mukumvetsera mawu ache. Ntchito yochitira kunyumba ithandiza inu kuti muchitepo kanthu. Chitani izi zonse molongosoka ndi kulemba mayankho mbuku lanu lolembamo (kope).

Khalani okonzeka kugawana ndi mphunzitsi wanu zomwe mwapeza mokamakakumana muphunziro lotsatira. Pa ndime iliyonse muli kuphunzira pali vesi la pa mtima. Kusunga pa mtima mawu a m'baibulo ndi madalitso pogwira ntchito ya Mulungu, ndipo ndikukulimbikitsani kuti muzichita izi. Koma ngati mupeza kuti ndi zobvuta mutha kusiya.Kwa iwo amene afuna kuyetsera, ndiganiza kuti choyamba alembe vesilo pa kapepala ndipo aliwerenge vesilo mbaibulo ndikuyamba kulinena vesilo pa mtima posayangánira mbaibulo. Likakhazikika, tengani lina ndipo muchite chimodzimodzi. Kumbukirani pomatchula chaputala komanso vesi: mwachitsanzo nunsu.

C. ZOFUNIKA KWA WOPHUNZITSA.

Ndakulandirani mmaphunzirowa monga wophunzitsa. Mwaitanidwa kugawana ndi anzanu zomwe mwakhala mukuphunzira njira ya Mulungu imene ndi yokoma komanso ikudalira inu kuti muchitepo kanthu. Dziwanoi kuti Mulungu akudalira inu ndipo akulimbikitsani ndi kukupatsani nzeru zimene zikukusowani kuti muphunzitse bwino. Tiyeni tigawane mfundo zothandiza kuti ntchitoyi ikhale ya phindu.

Pamene mukuphunzitsa wina monga pa tchalitchi, payenera kukhala wina wokuyanganirani pamene mukuphunzitsa. Ngati wachikulireyu sanasankhidwe, funsani akulu a mpingo kuti akusankhireni woyangánira ntchitoyi. Inu ndi wophunzira wanu muziona bwino ntchito yonse yomwe mukuthandizana,makamaka mukakumana ndi bvuto limene panokha simungalikwanitse.

Musanayambe ntchito yophunzitsa, werengani magawo onse a maphunziro anu ndi kuona mawu onse ofunika mbaibulo, kutsimikizira kuti mukudziwa choonadi chonse chomwe muphunzitse. Paulo ali ndi liwu kwa munthu wokhumba "kuphunzitsa achichepere"monga mmene aliyense aphunzitsira akhristu atsopano. "ndiwe tsono wakuphunzitsa wina, kodi ulibe kuziphunzitsa mwini?(Aroma 2:21) "Muyenera kumachita zimene inu mukuphunzitsa."

Pali magawo ena mmaphunzirowa amene ndi wobvuta pa moyo wanu wa chikhristu, ndipo dziwani kuti muzilumikizana ndi wophunzira wanu osati pa zokha zimene inu munena komanso pa zimene inu muli.

Palinso chinthu china chofunika kwambiri powerenga chiphunzitso chisanayambe. Simungathe kuphunzitsa chinthu chimene inu simunachimvetse bwino, ndipo mukambirane ndi wachikulire zobvuta zonse zimene mwakumana nazo powerenga. Izi nzofunikira kwambiri kuti musadodome pamene mwayamba kuphunzitsa. Chinthunso china chabwino ndi choti tchalitchi chanu chithanso kuphunzitsa onse amene ali woyenera kuphunzitsa ndi cholinga choti wophunzitsawo akhale ndi mwayi wodziwa ndi kuthandiza zobvuta zonse monga pagulu.

Kuti ntchito yophunzitsa anzanu ikhale ndi tanthauzo payenera kukhala ubwenzi wabwino pakati pa wophunzitsa ndi wophunzira. Mpangeni wophunzira wanu kukhala bwenzi lanu. Sichingakhale chobvuta kulandira malangizo ndi uphungu kuchokera kwa munthu amene amakukonda kwa thunthu. Onetsetsani kuti mwamudziwa bwino, mwadziwanso kubanja kwake ndi zomwe amakonda,komanso mbiri ya kutembenuka mtima kwake ndi zomwe zimamubvuta iye.

Kumudziwaku sikuonetsera chikondi chokha komanso kuthandiza inuyo kuti mudziwe chomupempherera ndi maphunziro amene angakonzedwe kuti amuthandize iye kukula mu uzimu.

Mungathe kukonza nthawi yodyera limodzi maphunziro anu asanayambe komanso mukhale ndi nthawi yoti iye akudziweni. Ndiponso adziwe mmene munalandirira Yesu

kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu. Pamene muchita maphunziro pamodzi, limbikitsani wophunzira wanu kupemphera monveka ngakhale pempherolo litakhala chiganizo chimodzi. Phunzitsani wophunzira wanu kulankhula ndi Mulungu njira ina ili yonse ndiponso mchilankhulidwe china chilli chonse.

Musanayambe phunziro latsopano, onani ntchito yonse ya kunyumba ya ophunzira wanu. Mulimbikitseni pokambirana pa zimene iye wapeza ndiponso zobvuta zimene wakumana nazo mphunzilo lapitali. Chofunika kwambiri ndi kudziwa ngati iye akuchita zimene ali kuphunzira.

Tsopano ndinu wokonzeka kuwerenga chiyambi cha phunziro ndi kuyamba kuphunzitsa. Kumuthandiza wophunzira wanu kuwerenga mawu mbuku lopatulika ndi kumvetsa zimene Mulungu akunena. Wonetsetsani kuti musataike chifukwa cha zinthu zina zosangalatsa. Izi zikhoza kukuonongerani nthawi. Gwiritsani ntchito nthawi yotsala pokambirana zimene mwaphunzira ngati nthawi ingapezeke.

Ndichofunika kukambirana zimene mumachita komanso zimene mwadutsamo pofanizira ndi mutu wa uthenga kapena ndemanga mphunzirolo. Muthanso kunena za zinthu zimene munakhala mukuzilephera ndi mmene Mulungu anakupambanitsirani. Mkhristu watsopano amazindikira komanso amalimbikitsika ndi zimenezi.

Pempherani kwambiri nthawi zimenezi pamodzi. Pemphani Mulungu kuti apitilize kukupatsani luntha lakutha kuphunzitsa choonadi cha mzimu wa chikhulupiriro kuti wophunzira wanu achilandirenso ndi mzimu wachikhulupiriro ndi kuyamba kuyenda mçhikhulupirirocho.

Mwina mwake nkhawa ya wophunzira imatha kuoneka yaikulu osadziwa kutichisomo chitha kugwira ntchito. Ndichofunika kumadziwitsa achikulire kawirikawiri mmene ntchito yanu ikuyendera.

Potsiriza, kumbukirani akhristu anzanu, atsogoleri ndi ena amene adatengapo mbali pa moyo wanu wa uzimu kuchoka ku dziko (mmoyo wochimwa) ndi kubwera kudzanja la Mulungu. Mulungu akugwiritsani ntchito kuti musogolere miyoyo ina ku ufumu wache. Ndi ntchito yabwino bwanji? Dziperekeni ku ntchitoyo mozichepetsa, ndi pemphero lonse ndi mokhuzidwa ndi Mulungu akhala nanu.

GAWO 1

KUBWERA MWA KHRISTU.

Phunziro 1-6.
Kale pamene munthu wafuna kuti akhale mgulu la zochika zina, panali zomuyenereza zina zoti azichite ngakhale iye asakufuna. Zina mwa zimenezi ndi zimene inu munazichitapo mwakufuna kwanu komanso mokakamizidwa. Pokhapokha mukakhala mmodzi wa gululo wobvomerezeka ndi aliyense ndiye titha kunena kuti "mwadzodzedwa"kukhala membala wa gululo. Chikhristu sichapafupi kwa aliyense.

Tingathe kunena kuti "kudzodzedwa mchikristu" Izi zimatheka ndi kubadwa mwatsopano (Yohane 3:3),kapena kubwera mwa Khristu. Mungathe kuona ngati mwachita kale zimenezi, koma nkofunikiranso kumvetsa bwino zinachitika kwa inu.

Palinso zimene sitingazilambalale, monga ubatizo wa mmadezi ndi kuzazidwa ndi mzimu woyera. Izi ndizofunika kwambiri pofuna kukhala mu ufumu wa Mulungu. Maphunzirowa akhazikitsa maziko a moyo wanu wa chikhristu. Mzonika kuti inu muzichite zimenezi.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO 1

KUSINTHA KWAKUKULU.

Baibulo limanena za kutembenuka, kupulumuka kapena kubadwanso mwatsopano. Pofuna kumvetsa Mulungu wachita pa moyo wanu muyenera kukumbukira mmene munalili mmoyo wanu kusanachitike. Kodi munachita bwanji?Nanga abale ndi abwenzi anakuonani bwanji?

Umo ndi mmene unu munalili. Tsopano tione zomwe Mulungu akunena za inu tsopano.Apatu tikunena za moyo wanu watsopano. Simunafike chimene mudzakhale komanso simuli monga mmene munalili. Chozizwa chachitika mwa inu. Sichifukwa cha ganizo lanu lofuna kukhala "mkhristu."Mulungu wakupangani kukhala munthu watsopano.

Ngakhale paliponse pa thuipi lanu sipanasinthe koma mkati mwanu mwasintha kwakukulu. Izi zili chomwechi chifukwa mwasinthika, mwayamba kukhala moyo watsopano wosinthikanso.”Kukhala njira ya Mulungu”

Maphunzirowa ali ndi mawu ambiri ochokera mbaibulo kuti muziwerenga. Musaope chimenechi. Maphunzirowa pa okha ndi osabvuta ndipo akuthandizani kudziwa mmene mungapezere njira yanu kedzera mbuku lopatulika.

PHUNZIRO1

KUSINTHA KWAKUKULU.

Werengani: 2 Akorinto 5:14-21.

Tchimo ndi zimene zimapangitsa : Ndi nthenda imene wina aliyense wakhuzidwa nayo (Aroma 3:23) “kuperewera” kulingati kusafikira pa mulingo . “Kuphonya kuli ngati ndime imene.” Tonse talephera kufikira pa muyeso wa ulemelero wake wa Mulungu umene umatchedwa ülemelero wa Mulungu”(Yesaya 64:6) Anthu siwochimwa chifukwa cha uchimo koma tchimo linawapangitsa anthu kukhala wochimwa; mwachitsanzo, timabadwa mphulupulu (Masalmo 51) Monga nkhosa tonse tasokera……(Yesaya 53:6). Mfundo yopambana ndikudziwa kuti zakale zapita zatsala zatsopano (2 Akorinto 5:17)

ZAKALE ZAPITA

Musanabwere kwa Khristu, inu munasankha ntchito za mdima. Inu munali otanganidwa ndi ntchito za oipayo(tchimo).Ndipo simunathe kuzikonza nokha. Baibulo limanena kuti:

1. **Munali wakufa** – Aefeso 2:1 Izi zitanthauza kuti simunamvere kapena kubvomereza, kapena kumkondweretsa Mulungu.

2. **Kudetsedwa** – Tito 1:15 zonse ziyera kwa iwo amene ayera mtima, koma kwa odetsedwa ndi osakhulupirira kulibe kanthu koyera.

3. **Kapolo wa tchimo** – Yohane 8:34 Osatha kumasuka. Ochita ukapolo wa zilakolako ndi zokondweretsa za mitundumitundu (Tito 3:3)

4. **Kuchititsidwa khungu ndi satana** 2 Akorinto 4:4. Ndi “kusatha kuona”choonadi cha Mulungu kuti choonadicho chikumasuleni (Yohane 8:32).

5. **Kuyembekezera chiweruzo cha Mulungu** Aefeso 2:36 pokhala ndi mantha, poyembekezera chilango cha Mulungu chifukwa cha uchimo umene wamkwiyitsa Mulungu.

6. **Kudulidwa kuchoka kwa Mulungu**. "Olekanitsidwa ndi Khristu"……Opanda Mulungu ……amene munali kutali (Aefeso 2:12-13). Ngati simunalape ndi kulandira Khristu; kulekanitsidwa kumeneku mathero ake ndi imfa ya muyaya (Aroma 6:23) imene ili gahena.

ZATSALA ZATSOPANO

Ngakhale umunthu wanu uzioneka chimodzimodzi, koma mwakhala "wolengedwa watsopano", munthu watsopano wa machitidwe atsopano. Ubale watsopano, maonekedwe atsopano ndi zolinga zatsopano mmoyo wanu,zokhumba zatsopano komanso abwenzi atsopano. "kusintha kwakulu."
Izitu zikutanthauza kuti:

1. **Kukhululukidwa** (1 Yohane 1:9a) Pamene Mulungu wakhululukira nthawi yomweyo amayiwala (Yesaya 43:25). Musalore chikumbumtima kuti chikutsutseni (Aroma 8:1,33-34). Bvuto lachotsedwa.

2. **Kulungamitsidwa** kapena kukhala opanda mlandu pamaso pa Mulungu (Aroma 3:24). Pa mtanda Ambuye Yesu anatenga tchimo lako kuti iwe utenge chilungamo chake (2 Akorinto 5:21) msinthano wopambana zedi!

3. **Kuyeretsedwa** chikumbumtima, malingaliro ndi machitachita zimayeretsedwa ndi mwazi wa Yesu (1 Yohane 1:7) Kodi sikwabwino kukhala oyera?

4. **Kuyanjanitsidwa** poyamba munali mdani wa Mulungu, tsopano ndinu bwenzi lake (Aroma 5:10) Simuzapezanso bwenzi lina loposa Yesu.

5. **Kubadwanso mwatsopano** Yohane 3:3…kubadwa mthupi monga mmene makolo anu alili kenako perekani moyo kwa Mulungu ndipo Mulungu akupatsani moyo watsopano umene iye akufuna kufikira ku moyo wosatha.

6. **Mbanja la Mulungu**. Mulungu tsopano ndi atate wanu, inu ndi mwana wake (2 Akorinto 6:18). Ichi chikutanthauza kuti okhulupirira onse ndi abale ndi alongo anu. Monga tate, ndiwotsimikiza kukukondani,kukutetezani,kukwaniritsa zosowa zanu ndiponso kukuphunzitsani zoyrnera mmoyo watsopano.

7. **Oyembekedzera ulemelero wa Mulungu**. Yesu Khristu anapita kukakukonzerani malo (Yohane 14:2,3) pakali pano ali kukonza malowo. Tiyembekedzere zabwino zili mkudza (1 Akorinto 2:9).

Zonse izi sizimene mlaliki amanena koma ndi zimene Mulungu mwini akunena kwa inu monga wokhulupirira weniweni.

Lowezani pa mtima

“Chifukwa chake ngati munthu ali yense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, zatsala zatsopano (2 Akorinto 5:17).Yetsetsani kuloweza vesili kuti muzitha kulakatula osayangánira.

Ntchito ya kunyumba.

1. Pa mutu wakuti “zakale zapita” pali kufotokozera kokwana kusanu ndi kumodzi (6) kwa moyo wanu wakale. Werengani mawu mukufotokoza kumodzi kumene mungasankhe ndi kutambasula nkhaniyo bwino lomwe ndi momveka bwino ndipo muilembe mu kope lanu.

   Kumbukirani kuti mmenemo ndi mmene zilili ndi anzanu kapena abwenzi anu amene alibe Khristu. Lembani maina awo onse ndipo muyambe kuwapempherera mmodzi mmodzi kuti Mulungu awapulumutse monga mmene inu munapulumutsidwa.

2. Pa mutu wakuti “zakhala zatsopano” pali kufotokoza kokwana kusanu ndi kuwiri (7) kofotokozera moyo watsopano. Pezani malo anu achete. Werengani mawuwo pa mfundo ili yonse mofuula potsatira mawuwo. Mwachitsanzo; ndinakhululukidwa chifukwa 1 Yohane 1:9 ikunena kuti tikabvomereza machimo athu; ali wokhulupirika ndi wolungama kutikhululukira ndi kutisambitsa ……..kenako lembani mu kope lanu mpakana mutsilize zonse zisanu ndi ziwiri musanapite kukafotokodzera wina. Potsiliza, thokozani Mulungu pokhala nanu mu nthawi imeneyi ndi madalitso a kusintha kwakulu mmoyo wanu.

Chiyambi cha phunziro 2

KUSANKHIDWA

“Khristu munampeza bwanji?”Wina anafunsa mkhristu.”sindinampeze Iye” linali yankho. Ïye anapeza ine!” Chipulumutso Mulungu ndiye amene amayamba. Iye ndiye amayamba kukufunafuna iwe usanayambe kumfuna iye. Makamaka zimakhala choncho, usanayambe kumfuna kapena kumdziwa Iye, Iye amakhala atayamba kale kugwira ntchito yofunafuna iwe.

Mungathe kuganiza kuti inu ndi amene munasankha Khristu, koma zimatheka chifukwa Iye anakusankhani inu poyamba.

Uwu ndiwo mutu wa phunziro lathu. Okhulupirira amalitcha “maitanidwe.”Mutha kudabwa kuti angakusankheni bwanji inuyo musanabadwe kapena inuyo kulibe. Kapena angakusankheni bwanji pamene Iye wakupatsani ufulu wa kusankha mwa inu nokha kumkonda ndi kumtumikira Iye.

Musabvutike chifukwa cha anthu ambiri amene amasokonezeka ndi zimenezi. Sichapafupi kumvetsa zimene Mulungu wachita pa miyoyo yathu kuti tipulumutsidwe. Tiyamike Mulungu chifukwa cha chinsinsi pa maitanidwe athu, potisankha kuti tisangalale ndi madalitso a chisankho chake, mwachidule tinene kuti Iye amatikonda ife.

PHUNZIRO 2.

KUSANKHIDWA.

Werengani: Deuteronomo 7:6-9

Mulungu anatenga gawo loyamba. Chipulumutso sichinayambe ndi munthu kufunafuna Mulungu koma Mulungu kufunafuna munthu nampeza. Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu anasankha anthu ake ndipo anwapatsa ufulu wonse wakuganiza ndi kusankha chochita. Ndipo anwachenjeza kuti pamene aphwanya malamulo ache ndiye kuti apalamula pamaso pache.

Chofunika kudziwa ndi chakuti; ngakhale ndi kobvuta kumvetsetsa, tiyenera kukhulupirira ngakhale ndi zobvuta kuzimvetsa.

MUNASANKHIDWA LITI?

Chisankhochi sichinachitike chifukwa cha mmene timaonekera kuti ndife woyenera chpulumutso! Chisankhochi chinachitika inu musanabadwe ndiponso musanachite chilichonse chabwino kapena choipa. (Aroma 9:10-12) chisankhochi chinachitika dziko lisanalengedwe (Aefeso 1:4).

KODI MULUNGU AMAONA CHIANI POSANKHA?

Popeza munasankhidwa musanabadwe osati chifukwa cha ntchito zanu zabwino; koma anatiyitana iye ndi maitanidwe oyera, si monga mwa ntchito zathu, komatu monga mwa chitsimikizo mtima cha Iye yekha, ndi chisomo chopatsika kwa ife mwa Khristu Yesu zisanayambe nthawi zosayamba (Tito 3:5; 2 Timoteo1:9). Munva zambiri zokhuza

chisomo mmaphunziro amenewa. Izi zikutanthauza kuti chikondi cha Mulungu chamangililika kwa iwo amene anali wosayenera kuchilandira. “Choperekedwa popanda dipo kwa iwo ndi wosayenera kulandira” Anakusankhani chifukwa chakuti Iye amakukondani inu. Chifukwa cha chikondi chimenechi, chisankho chake anasankha Israeli (Deutronomo 7:7).

NDINU MPHATSO YA CHIKONDI

Ndinu mphatso ya chikondi kuchokera kwa atate kupita kwa mwana (Yohene 6:37). Munadza kwa Yesu osati mwa kulingalira kwanu, koma atate anakukondani (Yohane 6:44). Palibe munthu angadze popanda kukonzedwa. Iyi ndi ntchito ya mzimu woyera.

MULUNGU SANADZIDZIMUKE NDI CHIPULUMUTSO CHANU.

Mwa nzeru zake Mulungu anadziwa zonse mmene anakusankhani inu(1 Petro1:2). Ma ukwati amachitika, kenako amazindikira bvuto lomwe akukumana nalo, nkhawa kuyamba kuwasautsa.Ngakhale ndinu wopanda mphamvu, wolephera ndi wochimwitsitsa. Mulungu anakufunani inu.Mwa khwimbi la wanthu, Iye anasankhula inu! Ndinu “woposa onse”, wosankhidwa.

PHUNZIRANI KUZIBVOMEREZA INU ENI.

Mulungu anasankha inu, kukulengani inu mchifanizo chake, ndipo anakuombolani inu. Musakhale pa zimene munthu ali, umunthu wake ngakhale mphatso zimene ali nazo. Pakukusankhani inu monga mwa umunthu wanu, anakuumbani mwa kufuna kwache. Palibe funso apa (Aroma 9:20).Mmalo mwake, muyamikeni iye chifukwa cha ichi (Masalmo 139:14).

ZIPHINJO ZACHOKA.

Sikofunika kuzimva, izi zidalira pa ine. Kodi ndapeza chimene chilli mmalo mwake? Zili mwa Mulungu amene anasankha ine, nandidziwa bwino kuposa umo ndimadzidziwira ndekha. Chisomo chake chikwanira mu zosowa zanga zonse(Yohane 1:16; 2 Akorinto 12:9)

MULUNGU ALI NDI DONGOSOLO LABWINO PA INU.

Chisankho chimachitika monga umo kalipentala amasankhila chida molingana ndi ntchito akufuna kuigwira. Mulungu sangangokusankhani kuti muzibvutika. Iye mwini amayamba wazifunsa kuti kodi ndichita naye chiyani munthu uyu.

Wakusankhani ndi cholinga, ndipo pamene inu munasankhidwa cholinga chake chinayamba kugwira ntchito (Aefeso 2:10). Mutha kukhala osadziwa dongosolo koma Mulungu adzabvumbulutsa dongosolo pangóno pangóno. Pamene dongosolo liyamba

kugwira ntchito, inu mumakhala otetezedwa, aphindu pokwaniritsa cholinga cha Mulungu.(Yohane15:6)

Lowezani vesili pa mtima.

Pakuti mwapulumutsidwa ndi chisomo cha kuchita mwa chikhulupiriro….chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu (Aefeso 2:8-9).

Ntchito ya kunyumba

Yankhani mafunso awa mu kope lanu.

1. Kodi ndi zodabwitsa ziti zachokera ku mfundo yoti Mulungu anakusankhani? Werengani Aefeso 1:4 ndi Aroma 8:29.
2. Tchulani zodabwitsa zinayi(4) zimene 1 Petro 2:9 akunena kuti anthu a Mulungu ali chifukwa cha chisankho chake?
3. Lembani zonse zimene inu mukufuna zofotokoza mmene Mulungu anakulengerani inu. Ndipo muuzeni iye kuti ätate zinthu zonse munazichita bwino ndithu."

Chiyambi cha phunziro 3

ZIMENE MULUNGU ANACHITA.

Mu phunziro lapitali, timanena kuti chipulumutso chimayamba ndi Mulungu osati inu. Anakusankhani inu ndipo amakukondani inu. Tsopano tiyenera kuganizira zimene iye wachita poonetsa chikondi pa chisankho chake kuti chikhale ndi tanthauzo.

Sitiganizira zambiri za zimene Mulungu wachita pokulenganinso kukhala wolengwdwa watsopano mwa Khristu. Chimenenso chitanthauza kuti "kusintha kwakulu"(phunziro 1). Koma chimene wachita kwa inu pokhala mpulumutsi wanu ndi chiyani?

Taganizirani za chipulumutso ndi ntchito yayikulu ya pa mtanda ndi tanthauzo lake. Ndikofunika bwanji kuti Yesu abwere? Nchifukwa chiyani adayenera kufa? Tingatsimikize bwanji kuti imfa ndi kuuka kwake kwatipindulira?

Ndikofunikira koposa kumvetsa izi. Masankhidwe a Mulungu pa okha sakadakusungani inu kwa Iye yekha. Kulekana kwa pakati pa inu ndi Iye, kunachotsedwa. Anapeza njira yakukuyeretsani pakati pa Iye yekha ndi Mulungu wa chilungamo ndi woyera.

PHUNZIRO 3

ZIMENE MULUNGU ANACHITA.

Werengani: Aroma 5:1-9.

Bvuto la tchimo

Mulungu anapanga munthu kuti akhale mchiyanjano ndi iye, koma tchimo linabweretsa udani (Genesis 3:8). Chiyanjano chingabwerenso bwanji? Pamene choyambitsa udani chinachotsedwa, munthu alibe mphamvu yochotsa udani umenewu.(Aroma 5:6).
Zitha kuoneka ngati kuti munthu yemwe akuyesa kuzinyamula pokoka zingwe za nsapato zake. Ndi Mulungu yekha angathane ndi bvutoli.

Kutha kwa bvuto.

Kudzera m'kukonda kwake anakusankhani inu, Iye sanawerengere tchimo lanu (Habakuku 1:13). Uchimo uyenera kulipidwa (uli ngati ngongole). Inu munalibe dipo la tchimo, choncho Mulungu analipira ngongoleyo.
Kodi Mulungu analipira bwanji?

Mwazi unayenera kukhetsedwa.

Pamene Mulungu anakonza za chipulumutso pochokera ku Aigupto, banja lililonse linapereka mwana wa nkhosa (Ekisodo 12:3) Izi zimalozera mwana wa nkhosa wa Mulungu (Yesu Khristu) amene adzaperekedwa chifukwa cha machimo a anthu (Yohane 1:29). Mulungu akutiphunzitsa kuti popanda kukhetsa mwazi palibe chipulumutso (Ahebri 9:22b). Lamulo la Mulungu litsimikizira kuti mphoto yake ya uchimo ndi imfa (Ezekieli 18:4)

Yesu yekhayo amene sanalawe tchimo, anazipereka, nazunzidwa kuti akapulumutse inu ku uchimo ndi kukubwezani kwa Mulungu (1 Petro 3:18a). Ndi mwazi wa Yesu wokha umene ungayeretse tchimo. (1 Yohane 1:7b).

Kuyeretsedwa ndi mwazi wake.

Kodi mwamvetsa liwu loti kuyeretsedwa mwaliwerenga kawiri mkhaniyi? Kuyeretswa ndi mchitidwe wa Mulungu umene tchimo lodetsedwa limayeretsedwa kukhala loyera.
Vesi 1 ikuti "tayetsedwa wolungama ndi chikhulupiriro". Iyi ndi mbali yanu ndipo tiyiona imeneyi mu phunziro lotsatira. Koma vesi 9 ikuti "popeza munayetsedwa wolungama ndi mwazi wake." Iyi ndi mbali ya

Mulungu. Kunena za kuyeretsedwa inu munalibe dipo, koma Yesu anadza kudzapereka dipo la tchimo lanu pa mtanda. Chiyero chake chonse chinalipira ngongole yanu.

Kodi mungatsimikize bwanji?

Chitsimikizo choti Mulungu wabvomereza kuperekedwa kwa Yeso Khristu kukuonekera mu kuuka kwa akufa (Aroma 4:25). Pamene munthu wamwalira, chuma chake chimasala ndi ena osiyidwa . Wakufayo sangachigwiritsenso ntchito.

Pamene Yesu anafa, anakusiyirani inu chuma cha chipulumutso. Naukanso kutsimikidzira kuti unu mwatenga chipulumutsocho (1 Petro 3:4). Tsopano ali kumwamba kuonetsetsa kuti chipulumutso chimene Iye anapereka pokuferani inu munachilandira? Ndipo muli nacho?

Chikondi chake - chibvomerezo chanu.

Mtanda wa Yesu ndicho chikondi cha Mulungu chimene wachionetsa (Aroma 5:8). Munthu amene anali mu bwalo lozengedwa mlandu anpezeka wolakwa. Woweruza sadamvere chisoni munthuyo chifukwa cha mlanduwo ndipo sunali wopepuka.
Iye adapereka chilango chokhwima. Mulungu woyera adapereka imfa monga dipo loombola tchimolo. Yesu analandira imfa ya pa mtanda mmalo mwa munthu wochimwa kuti mwazi wake utisuke ife tonse ku machimo athu.

Ichi ndiye chisomo nanga inu muchilandira bwanji? Isaac Watts, analemba nyimbo yopambana yoti chikondi chodabwitsa, choposa chikufuna moyo wanga, mzimu wanga ndi ine ndense.

Onani mmene Paulo analandira pa Afilipi 3:7-9.

Lowezani: Yohane 3:16.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero anapatsa mwana wache wobadwa yekha kuti yense wokhulupirira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha.

Ntchito ya kunyumba.

Yankhani mafunso awa:

1. Kufa ndi kuukanso kwa Yesu ; kumamukhazuka Iye pa mulingo wanji mmoyo wanu? (Aroma 14:9).
2. Mukuganiza kuti chitanthauzanji mmachitidwe? Mmayankho anu unikirani mmene moyo wanu ungakhuzidwire.

Chiyambi cha phunziro 4

ZIMENE INU MUNACHITA.

Mphunziro lapitali, taona mmene Mulungu anakhazikitsira chikondi pa inu pakukupulumutsani ku uchimo ndikukubweretsani kwa Iye.
Koma chipulumutso monga mudziwa, si ntchito imene Mulungu amachita payekha kwa ife, Zikufunika kumvomereza ndi kugwirizana naye.

Mkhristu amakambirana ndi wokonza sopo pa mfundo ya chikhulupiriro, “usa maganize kwambiri zaq chikhristu chako” ananena kwa mkhristuyo. Chakhalapo kwa nthawi yayitali koma taona zimene munthu akuchita lero lino. Pa nthawi imeneyi, anadutsa ana awiri ali kusewera mmatope mbali mwa njira. “sopo wanuyi bwanji? Wakhalapo nthawi yiposa chikhristu koma taona anawa ali bii koma sopoyo alipo.” Äh..” wopanga sopo anayankha. “sopo amagwira ntchito pokhapokha pamene munthu amugwiritsa ntchito.” Ndi zoonanso kuti chikhristu chimagwira ntchito ndi munthu wochidziwa.

Mu phunziro limeneli, tiona ntchito imene Khristu wachita kwa ife. Ndichofunika kwambiri kuunikira pa zochitika zathu.

PHUNZIRO 4

ZIMENE INU MUNACHITA.

Werengani : Machitidwe 20:17-21.

<u>Chiyambi.</u>

Ngati Khristu anafera onse, chifukwa chiani onse sanapulumutsidwe? Nanga chipulumutso nchokwanira kwa aliyense? Ndichokwanira, ndipo chimagwiradi ntchito kwa iwo ochibvomereza nthawi yabwino kuchokera mu uthenga wabwino. Kumbukirani woweruza amene anaperteka chilango chokhwima kwa bwenzi lake uja.

Chikanachitika nchiyani ngati wozengedwa mlandu sanasamale za dipo lake? Ntchito imene Mulungu anachita ndiye chipulumutso. Uthenga wabwino umatsimikizira mbali imene ife tiyenera kuchita pa chipulumutso. Tiyenera kuchita zimene Mulungu akunena mu Afilipi 2:12-13.

Kuchita mwa chifuniro.

Umunthu, malingaliro ndi chifuniro zimagwirira ntchito limodzi. Pamene munthu walandira uthenga wabwino, mmaganizo ake akhoza kusangalatsidwa, umunthu wake kugwedezeka koma chifuniro chake osasunthika. Oteroyo sangapulumutsidwe. Mwana wolowerera ananena, “ndizanyamuka kupita kwa atate wanga”Luka 15:18) apa ndi pomwe anatembenukira mmoyo wake.

Iye wofuna atenge chibvumbulutso 22:17 kutembenuka ndi kukhumba kwa chifuniro kuonetsedwa kudzera kukulapidwa kwa machimo, ndi chikhululpiriro kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi kuulula kudzera kwa anthu. Tiyeni tione mozama zinthu zimenezi:

Kulapa.

Kubwerera kwa Mulungu pa kulapa (Machitidwe 20:21) Liwuli limatanthauza kusintha kwa zinthu ndi chikhulupiro pa mbuye wathu Yesu Khristu.Makamaka kusintha kwa maganizo. M’malo mokana kapena kumsiya Mulungu, timatembenukira kwa Iye pomubvomereza monga mmene Iye alili.Ichi chitanthauza kusintha kwa maganizo athu, kuti ndife wochimwa ndipo tiyenera kulandira chipulumutso.

Ichi ndi choposa kungonena kuti ndalephera kapena ndalakwitsa. Ndi kusintha kwa maganizo komwe kungatithandize ife kusinthuratu maganizo athu. Tiyenera kuonetsa zipatso za kuyenera kutembenuka mtima (Mateyu 3:8).

Kulapa ndiko kubvomereza machimo athu kwa Mulungu ndi kuwakana kwathunthu machimowo (Miyambo 28:13). Ngati talakwira ena, tiyenera kubvomereza machimo athunso kwa iwo. Zimene taononga tiyenera tikonze; mwachitsanzo ngati zili ndalama tizibwenze ndi chiongola dzanja, katundu amene tinawatengera ena timubwenzenso ndi chiongola dzanja (Luka 19:8).

Chikhulupiriro.

“Khalani ndi chikhulupiriro cha cholinga kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.”(Machitidwe 20:21) Anthu ambiri amakhulupirira “zochita zawo zabwino” Kodi ndi Khristu? “Ndikhulupirira choncho, ndimachita bwino kwambiri.”

Izi zimalimbikitsa kunyada. Chipulumutso ndi mphatso, simalipiro kapena mphotho (Aroma 6:23). Chipulumutso ndi mphatso ya kwa Mulungu imene timalandira osati chifukwa cha ntchito zomwe timachita. Chikhulupiriro sikungobvomera mmaganizo. Kukhulupirira za Yesu si kukhulupirira Yesu.

Wina akhoza kunena kuti ndumakhulupirira za satana koma sindimamkhulupirira satanayo. (Yakobo 2:19). Kukhulupirira Khristu ndi chinthu chamtima kuposa cha m’mutu (Aroma 16:10) ndipo chithandiza ine kuzikhuthula kwa Iye kwa thunthu.

Ngati sindifuna kuzipereka kwa Yesu kuti azindilamulira ine, ndiye kuti sindimkhulipirira Iye. Chikhulupiriro chenicheni chimamufikitsa munthu kufika poitanira pa dzina la Ambuye (Aroma 10:13).

Kumvomereza

Kumvomereza Khristu ndiko kuuza ena adziwe kuti Khristu ndi mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wako (Aroma 10:9-10). Ichi chimathandiza kuti osakhulupirira alandire chipulumutso chawo. Pamene munthu wochimwa amvomereza Khristu pamaso pa anthu ena, Yesu amamvomereza iye pamaso pa Mulungu (Mateyu 10:32).

Lowezani.

Wobisa machimo ake sazaona mwayi, koma wakumvomereza, nawasiya adzachitiridwa chifundo (Miyambo 28:13).

Ntchito ya kunyumba

Baibulo likuti “khazikitsani maitanidwe ndi masankhidwe anu (2 Petro 1;10) ndipo dzifufuzeni ngatu mulu mchikhulupiriro (2 Akorinto 13:5). Izi zimalimbikitsa chikhulupiriro chathu ndiponso zimatipulumutsa nkuganiza kuti zinthu zili bwino pamene zisali bwino.

1. Fufuzani moyo wanu wakale musanabwere kwa Khristu, ndipo muzifunse kuti, kodi ndaulula ndi kuchotsa machimo anga onse? Itanani chisomo cha Mulungu kuti chichotse ndi kukonza Madera onse a moyo wanu mpemphero.

2. Dzifunseni nokha, ‘ndazipereka moyo wanga kwathunthu kwa Khristu?
   Iyedi ndi Mbuye wa dera lililonse la moyo wanga? Koteronso pempherani kwa Iye Madera amene mukuona kuti Yesu Khristu sakuwalamulira mmoyo wanu.

3. Ngati pali kulimbana kwina mmoyo wanu, dziwitsani nkhaniyi kwa mphunzitsi wanu kuti mukambirane za bvutoli ndipo mukatha mupemphere kuti lichoke. Tsimikizani kuti Mulungu wakusankhani kuti mukhale mfulu pamaso pake.

Chiyambi cha phunziro 5.

UBATIZO WA MADZI.

Tsopano tatsiliza phunziro lathu la ntchito ya Mulungu mwa ife yotchedwa “kubadwa mwatsopano.”Komanso pali zina zomwe zili za pa mfundo yomweyi ya kubwera kwa

Yesu, Ndi zofunika kwambiri kupereka moyo wathu watsopano kwa Khristu. Choyamba ndi ubatizo wa madzi.

Ngakhale zimaoneka zapafupi monga mwambo chabe wa chikhristu, ubatizo ndi chitsimikizo chopasmbana kwambiri kwa ife. Sichionetsa kubwera mwa khristu kokha komanso chimabweretsa chikhulupiriro cha mtsogolo mmoyo wathu. Kuti tikhale kuyambira tsopano mu mdalitso wathunthu mchipulumutso chathu.

Madera ena amene chikhristu kulibe satha kuzindikira pamene munthu akutsimikizira za chipulumutso mwa Khristu koposa pamene abatizidwa mtsutso umathera pomwepo.
Aliyense amakhulupirira kuti ubatizo ndi chizindikiro cha kunja kwa thupi koma chimaonetsa kutsimikiza mtima kwako.

Ukamawerenga makalata mchipangano chatsopano, sitimamva kuti okhulupirira akukakamizidwa kubatizidwa. Koma ndi dongosolo lache ndithu kuti ubatizo uchitike pamene munthu wabadwanso mwatsopano. Sitizapeza mkhristu wosabatizidwa mchipangano chatsopano.

Ngati inu simunabatizidwe, phunziroli likuthandizani kumvetsa bwino kuti ubatizo ndi lamulo la Yesu Khristu, ndipo tiyenera kulimvera. Ngati munabatizidwa, likuthandizani kumvetsa ubatizo bwino ndi zomwe zimachitika komanso zotsatira zake.

PHUNZIRO 5

UBATIZO WA MADZI.

Werengani: Aroma 6:1-11.

Chiyambi.
Chifukwa cha chisokonezo komanso kusamvetsetsana pakati pa akhristu pa nkhani ya ubatizo. Ndikufuna timvetsetsane bwino bwino monga baibulo limaphunzitsira za ubatizo.

Sitonena kuti mpingo umaphunzitsa bwanji za nkhaniyi koma tigwiritsa ntchito uthenga, mawu a Mulungu (Agalatiya 4:30). Musasokonezedwe kapena osazunguzika koma tikhulupirire uthenga okha. Amatiuza mmene ubatizo umachitikira komanso tanthauzo lake.

Kodi ndimakanda kapena okhulupirira ayenera kubatizidwa?

Makanda mwa Khristu okha basi ndi amene amabatizidwa mu nthawi ya chipangano chatsopano osati ongobadwa kumene monga atsopano mwa Khristu ayi.

Anthu obadwanso mwa Yesu ubatizo uchitike pamene munthu walapa ndi chikhulupiriro (Marko 16:16; Machitidwe 2:38). Munthu ayenera kubatizidwa pokha pokha wayamba waphunzitsidwa (Mateyu 28:19).

Kumizidwa m'madzi.

Ubatizo tanthauzo lake ndi kumizidwa mmadzi thupi lonse. Mchipangano chatsopano, okhulupirira onse anabatizidwa pomizidwa mmadzi ambiri.
Yohane anapeza pa malo pomwe panali madzi ambiri kuti agwire ntchito ya ubatizo (Yohane 3:23). Ichi chikutsimikidzira ubatizo wa yesu. Pamene Iye anabatizidwa "anatuluka mmadzi"(Marko 1:10).
Chimodzimodzi Filipo ndi mdindo uja (Machitidwe 8:38-39).

Ndani akuyenera kubatiza?

Munthu yekhayo wobvomerezeka, woyenera kugwira ntchitoyo osati aliyense. Mbusa ndi munthu woyenera kugwira ntchitoyi. Yesu sanabatize koma anapereka mmanja mwa ophunzira ake (Yohane 4:2).

Ngati wokhulupirira angathe kuphunzitsa wina, angathe kuikidwa kukhala wobatiza pokhapokha ngati mbusa palibe (Mateyu 28:19).

Paulo mtumwi anabatizidwa ndi amene ananenedwa wophunzira (Machitidwe 9:10-18).

Zikutanthauza chiyani?

1. Ndalowetsedwa Ubatizo ndi mwambo wolotsedwa (kukhala mmodzi wa gulu). Sitimabatizidwa "mchipembedzo"koma mwa Khristu (Aroma 6:3). Ndi thupi lake limene ndi mpingo.

2. Ndasindikizidwa ndi chizindikiro chimene chikhala cha mdulidwe chimene Abrahamu anadulidwa nacho chisindikizo cha chilungamo (Aroma 4:11). Ichi chiyenera kuvomerezeka ndi kulumbikitsa chikhulupiriro chako. Tiyeni tinene chomwechi kuti inu ndi kalata ndipo Khristu ndi invulopu ya kalatayo.
Pamene munatembenuka mtima inu, munaikidwa mwa Khristu ndi kumatidwa. Umo mmene ubatizo umachitikira. Umakhadzikitsa inu wotetedzedwa.

3. Ndatsukidwa kusamba mthupi ndiko ukhondo. Kutembenuka mtima ndiko kutsukidwa mwa kubadwanso mwatsopano (Tito 3:5) kumene kumathana ndi uchimo. Ubatizo umatikumbutsa kuti tsopano tayeretsedwa kapena kuti tikukhala mmoyo wa chiyero.

Werengani mawu ananena Hananiya kwa Paulo pa Machitidwe 22:16. Mawuwa akuluzanitsa ubatizo ndi kubadwanso mwatsopano pamodzi.Tisawasiyanitse. Pamene mwabadwa mwatsopano ngati simunamizidwe mmadzi, ndinu woyenera kubatizidwa.

4. Ndinabvomereza Khristu. Kubatizidwa kumakupatulani inu ndipo simungakhale ndi ubatizo wa pambali. Mchipangano chatsopano, ubatizo umachitikira ku mtsinje ndi malo ena mmatauni. Ubatizo sichinthu chofuna kudziwika ndi anthu ochepa. Chiyenera kukhala ngati ndandanda wa atsilikali amene abvala yunifolomu (Agalatiya 3:27). Simungabvale yunifolomu pamene muli msilikali wa chinsinsi.

5. Ndili mwa Khristu monga mwa kufa ndi kuuka kwake (Aroma 6:1-11).Tengani malo amene munabatizidwa ngati manda ndi thupi lanu ngati munthu wakufa. Chimachitika ndi chiyani ndi thupi lakufalo? Limakwiriridwa mmanda.
Munachita nawo chiani moyo kapena umunthu wanu wakale, popeza tsopano muli mwa Khristu? Unakwiriridwa njira ya ubatizo? Khristu anaukanso. Tikamachoka mmadzi nthawi ya ubatizo, timatsikimizidwa kuti taukitsidwa ndi Khristu chifukwa talumikizidwa naye kukhala mmoyo watsopano (Aroma 6:4). Khulupirirani chizindikiro chimenechi kuti ndi chenicheni mmoyo wanu.

Mathero

Ubatizo sichoonjedzera pa chipulumutso. Ndi chikakamizo cha Ambuye Yesu. Tsirizani vesili: Ngati mundikonda ine, mudza ……..
…… (Yohane14:15).

Lowezani

Kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa khristu Yesu tinabatizidwanso mu imfa yache? Chifukwa chake tinaikidwa pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa;kuti monga Khristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa Atate, chotero ifenso tikayende mmoyo watsopano (Aroma 6:3-4).

Ntchito y kunyumba.

1. Lembani mndandanda wa zotsatira za moyo wanu wakale zimene mukudziwa kuti sizingakhale gawo la moyo wanu watsopano mwa Khristu.
2. Bwerezaninso mndandanda ndipo ngati munabatizidwa kale muuzeni Mulungu chimodzimodzinso, kuti zakale zonse zinafa pamene munabatizidwa. Khulupirirani kuti Mulungu wakupangani kukhala mfulu.
3. Ngati simunabatizidwe, werengani Machitidwe 22:16 ndipo tsimikizani kumvera Mulungu. Tsopano tchulani zakale zonse za moyo wanu zomwe zili pz mndandanda ndipo khulupirirani kuti zonse muli kuzisiya mu mtsinje wa ubatizo.

Chiyambi cha phunziro 6.

UBATIZO WA MZIMU WOYERA.

Baibulo limatiphunzitsa kuti pali “ubatizo umodzi”mwa Khristu. Pakumizidwa mmadzi ndi gawo limodzi. Gawo lina ndi la ubatizo wa mzimu woyera(Yohane 3:5).

Ngakhale zinthu zambiri zasintha mmoyo wako kuyambira pamene unabadwanso, ukhoza kuonanso kuti pakusoweka mphamvu yakuchita umboni Khristu. Ophunzira a Yesu ngakhale adakhulupirira ndi kumkonda Iye, analinso choncho asanawasiye. Adawasiyira lonjezo la mzimu woyera kuti adzabwera pa iwo nawapatsa mphamvu. Zidachitika patangopita masiku ochepa Ambuye Yesu atakwera kumwamba.

Pa tsiku la pentekoste, anthuwa anasinthuka bwanji? Monga mtanda wa pa kalvari, pentekoste si nthano wamba kapena zochitika za pa mpingo, koma ndi zenizeni.
Tiyenera kulandira mphamvu ya ubatizo wa mzimu woyera monga mmene tidziwira mphamvu ya mtanda ndi chikhulupiriro.

Monga ubatizo wa madzi, si chinthu chongoonjezera ; koma ndi chimene Mulungu akufuna kuti ife tikhale pamene tayamba moyo wa Khristu mmene akhristu achitira. Phunziro ili ndi lo0njezano lodabwitsa limene Yesu anatipatsa, ndipo liyenera kuchitika mmoyo wathu.

PHUNZIRO 6

UBATIZO WA MZIMU WOYERA.

Werengani: Machitidwe 1:1-9.

<u>Kulongosola za mzimu Woyera.</u>

Nditsimikiza kuti mwakumana naye kale mzimu woyera! Chipulumutso chanu ndi madalitso amene atsatira ndi ntchito ya mzimu woyera. Ngati tilibe mzimu woyera, sindife akhristu (Aroma 8:9).

Chimene Khristu anachita mwa ife, tsopano mzimu woyera akuchita mwa ife. Si mphamvu ya Mulungu yokha, komanso mzimu woyera ndi munthu. Tidauzidwa kuti tisamukhumudwitse Iye (Aefeso 4:30). Ndipo sikungatheke kukhumudwitsa mphamvu. Mzimu woyera ndi Mulungu (2 Akorinto 13:14). Ndi chifukwa chache tilankhula za mzimu woyera monga “Iye “osati “iyo.” Tsopano tikambepo za mzimu woyera.

Kodi mzimu woyera nchiani?

M'baibulo timawerenga za kutsika kwa mzimu woyera pa anthu (Machitidwe 1:8),kudzazidwa kwawo ndi mphamvu (Luka 24:49). Kulandira (Agalatiya 3:2) kapena kusundikizidwa chidindo ndi mzimu (Aefeso 1:13). Tilandiriranji mzimuyo ngati tsopano tili naye? Kulandira kutanthauza kulandira kwatunthu ndi mphamvu.

Kodi kamodzi kakwana?

Sitilandira ubatizo wa madzi sabata ndi sabata chimodzimodzinso ubatizo wa mzimu. Koma ubatizo tidalandira uja umafunika mphamvu kuonjedzera kumene kumatchedwa kudzodza kapena kudzadzidwa. Tingathe kumadzazidwa kapena kumadzodzedwa koma ubatizo titalandira kamodzi kokha. Petro anadzodzedwa kawiri itafika nthawi ya pentekoste (Machitidwe 4:8, 31).

Mmene Ambuye wathu ananenera.

Yesu sanangokhala ndi chidziwitso chokha koma ananenedwa kuti munthu wodzala ndi mzimu (Luka 3: 21-22). Mitsinje ya madzi amoyo idzatuluka mwa iye (Yohane 7:38). Munthu wodzadzidwayo amabweretsa madzi amoyo kwa ena ndi kuthetsa ludzu lawo. Mulungu akufuna inu mukhale chomwecho.

Ntchito za ubatizo wa mzimu.

Mukalandira ubatizo uwu, mzimu woyera adzakuthandizani inu ku:

- Kukhazikitsa maziko eni eni a Yesu mmoyo wanu (Yohane 15:26)
- Kukupatsani mphamvu yakuchitira umboni za Yesu (Machitidwe 1:8)
- Kuwerenga baibulo lanu ndipo lidzakhala la moyo mmoyo wanu (Yohane 16:13).
- Kuti pemphero lanu likhale lochita chita (Aroma 8:26).
- Kutsogolerani pa machitidwe anu (Aroma 8:14).
- Adzakumasulani makamaka mmatamandidwe ndi mmayamiko (2 Akorinto 3:17).
- Kukudzodzani inu ndi chikondi cha Mulungu (Aroma 5:5) ndi chimwemwe (Machitidwe 13:52).
- Kukupatsani inu mphatso za mzimu (zida za mphamvu) kuti mugwiritse ntchito mu mpingo wa Mulungu (1 Akorinto 12:8-11).

- Kukupatsani mphamvu yosachimwa (Aroma 6:15). Zingathe izi kuchitika kamodzi kokha koma zikhala za inu ku nthawi zonse.

Kutumikira thupi

Cholinga cha ubatizo wa mzimu sikukuthandizani inu kuganiza kuti ndinu munthu wopambana ayi, koma kukupatsani mphamvu yakutumikira thupi la Khristu (1 Akorinto 12:7).

Thupi la munthu lili ndi magawo ambiri, gawo lililonse limachita ntchito yache; choncho ndinu gawo limodzi la thupi la Khristu kuti mutumikire pa ntchito imene wailonga mwa inu.

Kumbukirani phunziro 3 za masankhidwe anu. Mzimu woyera adzakukudzodzani ndi mphatso zimene inu muzifuna. Ndi chinthu chofunika kwambiri kutumikira (1 Akorinto 12:12-13).

Phazi langa ndi lofunika kwambiri monganso mmene dzanja lili. Sikuti okhawo amene ali ndi mphatso aposa ena ayi, koma tonsefe mu umodzi titumikire pa thupi la Khristu (1 Akorinto 12:21-220.

Malandiridwe a mzimu woyera.

Ngati munthu ali ndi ludzu, adze kwa ine amwe madzi …….Pa ichi Yesu amatanthauza Mzimu woyera umene anthu okhulupirira adzalandira (Yohane 7:37-39). Anakupatsani inu zinthu zitatu zoti muchite.

1. Ludzu…..kukhumba Mulungu ndi mtima wonse (Masalmo 42:1). Mulungu amapatsa ludzu komanso amachotsa ludzulo (Mateyu 5:6). Ngati inu mulibe ludzulo, mfunseni Mulungu kuti chifukwa chiani?
Ngati mwazadzidwa, dziwani kuti ludzulo ndi lofuna kutumikira nalo Ambuye Yesu.
2. Bwerani…..kwa Yesu amene adzakubatizani inu ndi mzimu woyera mukamupempha Iye (Luka 11:13).

3. Kumwa……Chikunthauza kugwitsa ntchito madalitso ndi chikhulupiriro. Yesu ananena kuti "chimene inu mupempha mpemphero, khulupirirani kuti mwalandira ndipo muzakhala nacho (Marko 11:24). Kupemphera sikungatheke opanda chikhulupiriro.

4. Kusanjika manja ….. ndi utumiki wokuthandizani inu kulandira. Munthu wosanjika manja amakhala mlumikizi amene mzimu amadzeramo kupita kwa munthu wolandirayo. Mphunzitsi wanu ndi wokonzeka kupemphera nanu motere. Yembekezerani kudzadzidwa ndi mphamvu ya Mulungu yotere. Yembekezerani kulandira malilime atsopano. Yembekezerani mitsinje ya madzi amoyo kuyamba kutuluka mwa inu.

Lowezani

Komatu mudzalandira mphamvu mzimu woyera atadza pa inu ndipo mudzakhala mboni zanga kuyambira ku Yerusalemu, Yudeya yense, Samariya kufikira kumalekezero a dziko (Machitidwe 1:8).

Ntchito ya kunyumba.

Pa mutu wa ntchito za mzimu woyera, pali zinthu khumi zomwe mukuziyembekedzera kuti zichitike mmoyo wanu. Lembani zomwe sizikuchitika ndi mawu ake ochokera mbaibulo. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni kuti zikhale gawo lanu. Kumbukirani kuti kukhulupirira ndiko kulandira.

GAWO 2

KUYENDERA LIMODZI

(Kuyambira phunziro 7 mpaka 13).

Mwaona kuti nkhani ya kubwera mwa Khristu kwambiri ikukhuzana ndi chisankho cha pawekha. Mzimu woyera wakuonetsani inu zofunika, kubvumbulutsa Yesu Khristu kwa inu ndi kubweretsa inu pa kulapa mwa chikhulupiriro. Sizikadatheka popanda wina kukutsogolerani. Koma pamene mwabadwanso mwatsopano muli mbanja la Mulungu, mpingo kuti muthe kukhala pamodzi ndi kukhulupirira ena.

Pamene munthu walowa mgulu la nkhondo , ayenera kutsimikizira ndi maganizo ake. Chitsimikizo chimenechi ndicho chitsogolere kulowa kwake mgululi. Pamene inu mwakhala mkhristu, muli mgulu la nkhondo la Ambuye Yesu.

Ubale wanu ndi Mulungu tsopano ndi woposa. Muphunzira zambiri mu gawo 3 la maphunzirowa. Koma mu gawo limeneli, tikufuna muganize zotsangalatsa ndi zofunikira za kukhala pamodzi mbanja la Mulungu.
Kukula kwanu mchikhristu kutheka kudzera mu ubale wanu ndi wokhulupirira anzanu. Izi sizitheka chifukwa cha zomwe atsogoleri anu anakuphunzutsani koma zimene inu mungagawane ndi iwo, chifukwa zikuthandizani inu kukula mu uzimu.

CHIYAMBI CHA PHUNZIRO7.

THUPI LOZIPEREKA.

Kodi mukamva munthu akunena za “mpingo” inu mumaganiza bwanji? Kukhala malo otopetsa pa chipembedzo pamene ena akusangalala? Kuimba nyimbo zomvetsa chisoni? Kumvetsera uthenga wotopetsa? Konzekerani zonse kukhala zatsopano.

Mpingo weni weni suli chomwecho. Pafunika kudzipereka osati kungopita ku chipembezo kamodzi pa sabata koma kuzindikira chisangalalo chokhalira pamodzi ndi akhristu ena.

Ndi nthawi yofunika kuti mukwaniritse zinthu zoti simunadzidziwe pachiyambi. Pamene mufufuza zinthu zenizeni, simulola kusiya zina padera.

PHUNZIRO 7.

THUPI LOZIPEREKA.

Werengani: Mateyu 16:13-20.

<u>Mpingo ndi chiyani?</u>

Gulu la anthu amene amazipereka ndi amene apeza umodzi watsopano ndi Mulungu. Simungathe kukhala mgululi popanda kubadwanso mwatsopano. Chipangano chatsopano chimanena kuti Khristu ndiye mutu wa Eklesia monga thupi lake (Akolose 1:18……monga anthu amene amakhala mmoyo wa Khristu ndi chitetezo chake. Monga ziwalo za thupi zosiyana, chomwecho ife amene tikhala mwa Khristu ;tisiyananso.Tiganize za mpingo mmagawo awiri:

1. <u>……ndizamanga mpingo wanga…Mateyu 16:18.</u>

Akutanthauza mpingo wa pamalo ponse umene Yesu anaufera (Aefeso 5:25). Okhulupirira onse, osayanganira mtundu, chikhalidwe, ukale kapena tsopano. Muli umodzi umene suoneka ndi maso. Kumanani ndi aliyense mwa Khristu posatengera mtundu wa munthu kapena chikhalidwe chake.

2. …….Uuze mpingo….Mateyu 18:17.

Izi zikutanthauza gulu la anthu amene amasinkhana pamodzi kaya kumizinda, kumidzi (1 Akorinto 1:2; Aroma 16:5). “Ndi gulu la anthu ozipereka” (mpingo). Mchipangano chatsopano ndi anthu obadwanso mwatsopano osati anthu achipembedzo.
Sizikutanthauza nyumba yopemphereramo. Yesu analonjeza kuti pamene mpingo ukumana pamodzi, Iye adzakhala pakati pawo (Mateyu 18:20).

Nanga magulu a zipembezo bwanji?

Izi zabwera chifukwa cha kugawikana kwa mpingo zimene panalibe pachiyambi ndi Mulungu. Yesu anakhazikitsa mpingo “thupi limodzi”(Aefeso 4:4)pamene chikhristu chenicheni chimamangikapo. Kumvera kwanu kwa Khristu ndi chinthu choyamba mu mpingo wake wa pamalo ponse kenako mpingo umene inu mukupembedza kumudzi kwanuko.

Tsegulani mtima wanu wokhulupirira onse ndikumawapempherera (Aefeso 6:18). Musaleke ichi. Tsiku lina onse adzakhalanso pamodzi.

Kodi mkhristu ayenera kukhala yekha?

Kodi akhristu alibe mpingo? Tangoganizani kuti dzanja likufuna kuchita zinthu palokha popanda kugwizana ndi mutu. Ziwalo zina zonse zitangochita chimodzimodzi, mathelo ake, zikhoza kufooka ndi kufa. “Mpingo” si kukumana kapena zochitika pa gulu koma ndi chiyanjano ndi Mulungu.

Chipangano chatsopano sichinenena kuti uzipita kutchalitchi ndipo ukakhale mkhristu wabwino. Chikunena mosiyanasiyana “akhristu ndinu ziwalo zimodzi mwa Khristu wina ndi mzake.(Aroma 12:5) ndinu chimango chimodzi mwa Khristu (Aefeso 4:2-3).

Kupereka ndi kulandira.

Umu ndi mmene mpingo ulili. Ukafuna kulandira kwambiri, uziperekanso kwambiri. Apa sitiyenera kupereka ndalama zokha. Izi ndi zimene Yesu adanena (Luka 6:38). Yambani kufunsa “nchiyani ndingapereke?” osati phindu lake nchiyani? Choncho muzapindula koposa pa zimene mwadzala.

Mwina mutha kuzifinsa, kodi ndingapereke chiyani? Tiyankha mafunso amenewa bwino lino mu gawo lomwe lino. Choyamba ndi chofunikira ndi kudzipereka kwanu (2 Akorinto 8:1).

Kudzipereka ndi mtima wonse.

Gulu losewera mpura limapambana pamene lazipereka kwathunthu pamodzi ndi wochemerera amene. Ichi ndi chimene Khristu akuyembekezera kwa ophunzira ake

(Luka 14:33). Iye anzipereka pa imfa ya pamtanda chifukwa cha ife (Agalatiya 2:20). Tangoganizani nzanu wokondedwa kunena kwa inu “ndimakukondani kwambiri koma thupi lanu lonyansa.” Izitu sizingatheke ndipo wozimva sangakhulupirire.

Malingaliro anu enieni kwa Khristui amatsimikizidwa ndi chikondi chimene mumaonetsera ku mpingo umene lili thupi lake. Simungathe kuzipereka ku mbali imodzi kwinaku osadzipereka (Mateyu 25:40; 1 Yohane 4:20)

Kuzipereka kumatanthauza kukhulupirika

(a) Kukhulupirika mmisonkhano …kumalimbikitsa abale ndi alongo (Ahebri10:25).
(b) Kugawana ndi abale za moyo wanu, mphatso zanu, chuma chanu komanso nthawi yanu (Ahebri 13:16). Kukhala limodzi mchiyanjano.
(c) Kudzipereka ku ntchito ya Ambuye …kumvera akulu ndi atsogileri amene ali abusa anu (Ahebri 13:17). Zambiri muphunzira patsogolo.

Lowezani

Pamene awiri kapena atatu akomana mdzina langa, ndidzakhala pakati pawo komweko (Mateyu 18:20).

Ntchito ya kunyumba.

1. Chipangano chatsopano chimatiuza kuti Khristi ndiye mutu wa Eklesia ndi thupi lake.(Akolose 1:18) Lembani mu kope lanu zimene mukuganiza kuti mawuwa akutanthauza? Werenganinso 1 Akorinto 12:14-27).
2. Mwaonanso kuti kukhala gawo la mpingo zitanthauza kuzipereka kwa okhulupirira anzanu. Lembani mu kope lanu zimene mukuganiza kuti kuzipereka kumeneku kukutanthauza kwa inu. Pemphererani mfundo ili yonse kwa Mulungu kuti akuthandizeni kuti muzipereke.

Chiyambi cha phunziro 8.

PHUNZIRANI KUKHALA PA CHIBALE.

Tkamanena kuti mpingo chomwe ungachite ndi kukhala pamodzi, zikutanthauza ubale. Potsiliza muona kufunika kwa ubalewu mu mpingo ndi ntchito zake. Koma mu phunziroli tiona kuti chikondi ndi simenti imene imagwiritsitsa nyumba pamodzi.

Zikumveka zabwino ndi zosabvuta mpakana mutayambapo kuchichita chikondicho! Mwina mwake mumaganiza za inu nokha, ngati wina aliyense angatenge kuti ndi zobvuta monga aganizira nokha; ndiye kuti simunayambe kudzidziwa nokha.

Koma potsakhalitsa, mudzidziwa pothandizidwa ndi akhristu anzanu. Mutha kukhala ndi mphatso inu osadziwa kuti muli nazo.
Muphunzira kukonda iwo monga mmene iwo ali. Chimodzimodzinso iwo adzakukondani. Ndi ubale woterewu umapangitsa kuti mpingo ukhale wolimba.

'Kukhala ndi oyera amene timawakonda mosakaika pamakhala ulemelero' 'Kukhala pansi pa oyera mtima amene tiwadziwa; Inde iyo ndi nkhani ina.'

PHUNZIRO 8.

KUPHUNZIRA KUKHALA PA CHIBALE.

Werengani : 1 Akorinto 13.

Chiyambi

Kodi mudakhumudwapo pamene wina ananena mawu osakusangalatsani? Sikuti ndi mawu osakusangalatsani amene anadzutsa mkwiyo **.** Kuphunzira kuthetsa bvutolo kumatenga mkwiyo kuti utsogole.
Pofuna kukhala ndi anthu ena amene Mulungu watipatsa, tiyeni timpemphe Ambuye kuti atithandize kukhala chikhalidwe chomwe anali nacho.

Kugwizana pamodzi

Kusunga umodzi wa mzimu kumathandiza mpingo kukhala wa mphamvu. Pamodzi tiima nji! Tikagawikana tikhala opanda mphamvu. Satana ndi mdani wamkulu, amalimbana ndi akhristu asaime pamodzi mwa mphamvu. Yetsetsani kusunga umodzi wa mzimu (Aefeso 4:3). Kodi mungachite bwanji?

Chikondi chimalimbitsa

Mpingo umaphatikiza onse. Akhristu anzanu ena amene inu simunawasankhe monga abwenzi anu koma Mulungu wawasankha kuti akhale abwenzi anu ndipo akusuleni inu.

Izi zimatheka mwa chikondi chimene chimangirira mpingo pamodzi osati mwa chikhalidwe kapena chikondi cha umunthu koma chikondi cha Mulungu.
Chikondi ndicho chikhalidwe cha Mulungu (1 Yohane 4:7-8). Pamene mzimu woyera anbwera kwa inu, Iye anabweretsa chikondi (Aroma 5:5).

Chikondi chiyenera kuonetsedwa

Sikungoganizira kokha, si mawu a pakamwa okha amene saonetsa ntchito (1 Yohane 3:18). Mnyamata amene wagwa mchikondi ndi mtsikana amene sanabvomereze chikondicho, amafunafuna njira zoti mtsikanayo avomere. Muyenera inu kuchita chomwecho kwa abale ndi alongo (Ahebri 10:24) mwa machitidwe oganiza bwino ndinso opanda khanza.

Chikondi chimayetsedwa

Sizochita zanu zokha komanso machitachita anu kwa anzanu ndi zimene iwo angakuchitireni inu. Apa ndi pamene chikondi chimayetsedwa. Sikukoma mtima kokha kwa iwo muwakonda, koma kuohunzira kukonda amene simuwafuna ndipo sangakuchitireni zabwino.

Izi zimathandiza kukumbukira :
(a) Mmene Mulungu wapirira
(b) Kuthanso kukhala ndi mtendere onse.
(c) Kumakonda kuganizira zolephera zanu ngati zochepa pamene za anzanu zazikulu koposa. Onani Mateyu 7:3-5.

Chikondi chimakululuka

Taganizirani mmene Yesu anaonetsera chikondi pa mtanda paja (Luka 23:34). Tikadatani ife popanda chikhululukiro cha Mulungu (Ahebri 10:17)? Mzimu wokhululukira ndi umene muyenera kukhala nawo mu mtima mwanu ngakhale munthu amene wakuchimwirani asanakupepeseni. Yesu amatiphunzitsa kuti ngati sitingakhululukire abale athu, tisayembekezere kukhululukidwa ndi Atate wathu wa kumwamba (Mateyu 6:4-15).

Zinthu zikasokonekera tichite bwanji?

Yesu anadziwa kuti nthawi zina zinthu zitha kusokonekera pakati pa okhulupirira, ndipo anatiphunzitsa mmene tingachitire mnthawi yotere.

1. Pamene wadziwa kuti bvuto ndiwe (Mateyu 5:23-24)

Pereka mphatso zako zimene zitanthauza kupemphera, kupembedza kapena kutumikira Mulungu. Ukafuna kuti Mulungu alandire mphatsoyo, yamba wathetsa mkanganowo ndi kuyanjana ndi mbaleyo usanapereke mphatsoyo kwa Mulungu

(Mateyu 5:23). Usanene kuti palibe kanthu! Ndingolapa kumbali yanga ndipo zinazo ndizisiya mmanja mwa Mulungu.

2. Pamene mukhulupirira kuti bvuto ndi la mzanu (Mateyu 18:15-17).

Pamene mukhulupirira kuti mwalakwiridwa, ndi chimodzimodzinso mmene mzanu angamvere mutamulakwira, Muklakwiridwa, ndi kobvuta kuteteza mkwiyo wanu pa inu nokha.
Pamene mungafune thandizo kuti wina alowere pa bvutolo zithandiza kubweretsa chiyanjano pamene mtendere wasowapo. Ngati woyambitsa ndi mzanu, tiyenera kupeza njira zina zothetsera bvutolo.

Mulungu sadakhazike inu pa dzikoli kuti mubwedzere choipa koma kuti munthandize wina kubwera kwa Yesu. Muyenera kukhala ndi mzimu wokhululuka ndi kukhumba kukhala ndi iye nthawi zonse.

<u>Ndani anatengapo mbali?</u>

Malingana ndi chiphunzitso cha Yesu, inu ndi amene mutengepo mbali pamene ubwenzi waonongeka. Ngati ndinu woyambitsa, yambani kuthetsa mkanganowo pomupepetsa ndi kuyanjana naye. Ngati ndi mzanu amene wayambitsa, musadikire iye kuti agonje kwa inu, koma pezani njira yothetsera.

Nanga mzanuyo achitenji? Nayenso ngati angathe kumvetsa bwino atha kutenga udindowo.

Lowezani

Khalirani okoma wina ndi mzake mtima wa chifundo, akukhululukirana nokha monga Mulungu mwa Khristu anakhululukira inu (Aefeso 4:32).

Ntchito ya kunyumba.

Pezani malo achete, tengani cholembera ndi kope lanu.

1. Lembani maina a onse amene simunawakhululukire. Pemphani Mulungu kuti akukumbutseni maina onse. Tsikimizani kukhululukira wina aliyense.Ndi zobvuta kukhululukira amene ali pafupi ndi ife monga akazi athu, achimwene, achemwali, abambo, amayi.

   Pempherani kwa Mulungu kuti akukhululukireni komanso kukupatsani mzimu wokhululukira kuti uchotse mkwiyo wonse ndi ululu wa mu mtima mwanu, ndi kukuzadzani ndi chikondi chake.

2. Pempherani kwa Mulungu kuti abvumbulutse amene inu simulankhula nawo chifukwa munayambana nawo. Pempherani kuti Mulungu athandize pochotsa bvutolo ndi kubweretsa chiyanjano.

   Pitani kwa mbale munamulakwirayo ndikumupempha kuti akukhululukireni. Ngati zingaoneke zobvuta, mulembereni kalata kapena muyimbireni fini yomupempha iye akukhululukireni ndi kuti pakhalenso chiyanjano pakati panu. Msimikizireni kuti tsopano ndinu wotsatira Khristu ndipo mwachita ichi pomvera mawu a Khristu.

Chiyambi cha phunziro 9.

CHAKUDYA CHA PANGANO.

Ubatizo wa madzi ndi chakudya cha Ambuye (mgonero) ndi zinthu ziwiri zoyenera kukumbukiridwa ndi kupatsidwa ulemu mmwambo wa chipembedzo. Tigwiritse ntchito madzi monga ku mbali yakuyamba chikhristu kapena kubwera mwa Khristu.

Tsopano tifuna kutenga mbali ya chiwiri imene tiitchula kuti “chakudya cha pangano” chimene tichifotokoze kwambiri mu gawo lino la chiwiri. Pofotokodzera zofunika kwambiri monga kuzipereka kwa wina ndi mzake ndiponso ubale wathu pamodzi mwa thupi la Khristu.

Pali mgwirizano pa mgonero wa Ambuye ndi ubatizo wa madzi. Zonsezi zilozera kwa Khristu ndipo zitikumbutsa ife zimene Khristu anachita pa mtanda. Zonsezi zikufotokozera zinthu zosiyana siyana pa mgwirizano wathu ndi Khristu mwa chikhulupiriro chochokera pa mtanda.

Uwutu ndi umboni umene wokhulupirira amanena za Khristu. Ngakhale zonse zili chomwechi, ubatizo wa madzi umachitika kamodzi kokha pamene mgonero wa Ambuye umachitika nthawi ndi nthawi, chifukwa timayanjanitsidwa ndi Iye.

Choona ndi chakuti, inu muli mwa Khristu. Zikupezeka mochulukirapo kawirikawiri mu utumiki wa Paulo mtumwi makamaka pa ubatizo wa madzi. Choona nchakuti Khristu ali mwa inu kukupatsani moyo wa uzimu ndi mphamvu,choonadi chimene chipezeke mu chakudya cha pangano.

PHUNZIRO 9.

CHAKUDYA CHA PANGANO.

Werengani: Luka 22:7-20.

Kuonetsedwa kwa chakudya cha mtsogolo.

Usiku umene Mulungu anatulutsa ana a Israeli mu Aiguputo, mwana wa nkhosa anaphedwa mnyumba ya m,Israeli aliyense. Ndipo mwazi wache unapakidwa pa mphuthu ya chitseko kupulumutsa banja lililonse kwa ngelo wa imfa. Ndipo nyama yache inaotchadwa ndi kudyedwa.

Chaka ndi chaka amakumbukira mwambo wa pasika pamene anapulumuka mu ukapolo. Nkhani imeneyi ikupereka chithunzithunzi cha mmene Mulungu anapulumutsira anthu ake ku machimo awo kudzera ku imfa ya Khristu pa mtanda.

Zikuonekanso chomwecho pamene tawerenga mu mutu wa 7 kuti Khristu ndi mwana wa nkhosa wa Mulungu amene anachotsa tchimo la dziko lapansi kutenga malo a nkhosa imene inaperekedwa nsembe ija.

Chinthu choyamba

Mmene Khristu mutu wa Eklesia amatiphunzitsa ndi kutipatsa njira monga Iye afunira; pali zinthu izi zofunika kuzionetsetsa;-

1. **Tsiku** : silinali loweruka kapena la Mulungu. Tsiku lina lililonse ndi lofunika.
2. **Malo** : chipinda china chilli chonse osati malo eni eni monga ku tchalitchi ndi amene ali ofunikira kweni kweni ayi.
3. **Zochitika** : ndi zinthu zina zitha kumachitika madzulo dzuwa litalowa makamaka chitachitika chiphunzitso.

Tanthauzo la mgonero

Zinthu ziwiri: mkate kuimirira thupi la Khristu. Ndi chikho cha vinyo kuimirira mwazi wake. Thupi lache linaperekedwa ku imfa ndipo mwazi wache unakhetsedwa kutipulumutsa ife.
Mkate umatiphunzitsa ife kuti tili ndi moyo mu imfa yache. Ndipo chikho chimatiphunzitsa ife kuti tinatsukidwa ndi kukhululukidwa mu mwazi wake.
Mwambo wa mgonero ndi:

1. Chikumbutso. Yesu ananena chitani chifukwa ndi chikumbukiro changa (Luka 22:19). Iye anafuna kuti ntchito ya pa mtanda ikhazikike mmaganizo athu. Ili ngati njira imodzi yonena zikomo Ambuye Yesu. Chikho chimatchedwa chikho cha mayamiko (1 Akorinto 10:16).

2. Kubvomereza. Okhawo anzipereka kwa Ambuye ali nawo ufulu wakukhala nawo pa mgonero wa Ambuye chifukwa anabvomereza Yesu kukhala Ambuye ndi mpulumutsi wa moyo wawo. Ichi chimatanthauza kuti inu mumalalikira imfa ya Khristu (1 Akorinto 11:26).

3. Kuyanjana ndi Khristu. Simukuyenera kumanoonerera anzanu ali kudya ndi kumwa koma inuyo osatengapo mbali pa thupi ndi mwazi wa Yesu (1 Akorinto 10:16). Pofuna kukhala ndi moyo wa Khristu, Iye anatiphunzitsa kuti tiyenera kudya thupi lake (mkate) ndu kumwa mwazi wake (vinyo)(Yohane 6:53-54). Zimachitika pa kutembenuka mtima koma chakudya cha lonjezo, chikutiphunzitsa ife kuti tiyenera kudya mkate nthawi ndi nthawi ndi kupeza mtendere wa moyo wa uzimu mwa Iye.

4. Pangano. Pamene mumawerenga Khristu anati, “chikho ichi ndi pangano latsopano limene lidzaperekedwa kwa inu (Luka 22:20). Simungathe kudya mgonero wa Ambuye pa inu nokha koma pamodzi ndi onse amene muli nawo mu pangano latsopano. Mkate umatanthauza thupi lake la Yesu lopachikidwa chifukwa cha ife, komanso moyo wake wa uzimu, mpingo, umene ife tonse tilimo(1 Akorinto 10;17). Pakudya mkate timakondwerera osati chifukwa tili nchipangano ndi Khristu yekha komanso ndi okhulupirira onse.

<u>Kuphunzira kuchokera ku Akorinto.</u>

Tsegulani 1 Akorinto 11. Paulo amadzudzula akhristu a ku akorinto chifukwa cha mmene iwo anayendetsera mwambo wa mgonero wa Ambuye. Ena amapita ali ndinjala pomwe ena ankapita ataledzera.

Pakuchita ichi amanyozetsa mpingo, kukhumudwitsa okhulupirira ena (vesi 21-22). Akhoza kudyera limodzi chakudya cha pangano koma mmalo molemekeza panganolo alikulikana.

Amazitengera mkwiyo wa Mulungu pa iwo wokha. Pachifukwachi ambiri anadwala, ena anamwalira chifukwa chakudya mgonero ali wochimwa (vesi 30). Pofuna kuti tisazitengere mkwiyo wa Mulungu, tiziyetse tokha ngati tili woyenera kudya mgonero wa Mulungu (vesi 28), ndi kuchotsa mphulupulu ina ili yonse pa thupi lathu kuti chiyanjano chathu chikhale bwino.

<u>Madalitso ndi Machiritso.</u>

Ndi zoziwika bwino kuti mgonero ndi njira ya chisomo. Chinapangidwa ndi Ambuye kutipatsa ife mdalitso. Palibe chikhalidwe china mu mkate kapena mu vinyo, ngakhale zitapemphereredwa ; koma I nuyo simulandira mdalitso ngati mudya ndi kumwa mulibe

chikhulupiriro mwa Khristu. Pakudya ndi kumwa mosayenera, Akorinto anadwala ndi kufa chifukwa cha mgonero wa Ambuye.

Zimatheka mukakhala okhulupirira, moyo wa Khristu umakhalanso moyo wanu. Akhristu a ku korinto anadwala ndi kumwalira chifukwa anadya mgonero wa Ambuye njira yolakwika.
Ndizothekanso kubwera pa gome la mbuye ndi chikhulupiriro ndi kulandira machiritso ndi madalitso a ku uzimu. Ngati mufuna madalitso ndi machiritso, yangánani kwa Mulungu chifukwa mukakhala pa chakudya, kuchokera mu imfa yake, machiritso amatumphukira kwa okhulupirira (Yesaya 53:4).

Zochitika zina pa gome la Ambuye pa nthawi ya mgonero.

Kunena za nthawi kuti tikhoza kudya kangati mgonero, Yesu anangati “muzichita izi”sananene kuti kangati. Pamene muli pa msonkhano, wokhulupirira akhoza kudya mgonero wa tsiku ndi tsiku.
Izi zimachitika pa nthawi ya pentekoste (Machitidwe 2:46). Amanyema mkate ngakhale mnyumba zawo. Izi zikuonetsa kuti amatha kudya chakudya cha Ambuye kwina kuli konse osati ku tchalitchi kokha ayi (1 Akorinto 11.
Baibulo sili tsimikiza kuti wodyetsa mgonero ndi m’busa yekha. Zikhoza kuchitika ngakhale a pa banja atatha kuchita mapemphero ndi anzawo.

Lowezani

Mukadya mkate wanu ndi kumwera chikho; mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akudza lye (1 Akorinto 11:26).

Ntchito ya kunyumba.

Gwiritsani ntchito kope lanu kuyankha mafunso awa;-

1. Munthu ayenera kuziyetsa yekha (1 Akorinto 11:28). Kodi mawu amenewa akutanthauza chiyani? Masalmo 139: 23-24 ikuthanduzani.

2. Ndi zinthu zanji zimene sizingakuyenerezeni kukhala pa mgonero?

3. Pamene mwakhala pa mgonero wa Ambuye ndi cholinga choti mulandire machiritso kapena madalitso mmoyo wanu wa uzimu.

(a) Ndi chokuyenerezani chiti chimene mungachikhumbe koposa kuti chikufikireni? (Werenganinso phunzirili kuti mupeze mayankho).

(b) Machiritso kapena madalitso mungawapeze bwanji?

Chiyambi cha phunziro 10.

ATSOGOLERI ANU.

Mulungu anakhazikitsa njira kuti akhristu tizipeza malangizo kuchoera kwa Mulungu, ndi kumtumikira Iye yekha. Koma Mulungu ali ndi njra zosiyanasiyana; amalankhula ndi ali yense payekha payekha komanso anakhazikitsa akulu akhale mmalo mwake. Ali ndi mbali yofunika yayikulu yotiphunzitsa ife chifuniro cha Mulungu.

Baibulo limafotokoza za anthu a Mulungu ngati gulu la nkhosa ndi atsogoleri ngati abusa. Timazilandira bwanji zimene Mulungu wakhazikitsa pa ife pofuna phindu kuti tikule mu uzimu.

Wokhulupirira aliyense ayenera kuphunzira kukhala pansi pa ulamuliro. Pamene taphunzira, ndi pamene tingpatsidwe ulamulirowo pa anzathu.

Mu phunziro limeneli tiphunzira za atsogoleri a mu mpingo, zimene iwo amchita, ndi mmene Mulungu akufunira inu kuti mukhale mu ubale ndi iwo.

PHUNZIRO 10.

ATSOGOLERI ANU.

Werengani: 1 Timoteo 3:1-12.

<u>Dongosolo la pa dziko.</u>

Ndi lamulo la Mulungu kuti gawo lililonse la moyo likhale ndi atsogoleri othandiza mu ulamuliro. Ulamuliro uli wonse umachokera kwa Mulungu, ngakhale maboma amasankhidwa ndi Mulungu (Aroma 13:1). Pamene ulamuliro ukusowa pali chisokonezo ndi zoipa (Oweruza 17:6).
Mu mpingo Mulungu anakhazikitsa atsogoleri ndi kuwapatsa ulamuliro wosamalira anthu ake. Tilankhulanso za mphatso za utsogoleri wa pa malo komanso woyenda yenda chifukwa awa ndi amene mungathe kukhala nawo pafupi ndi kugwira nawo ntchito.

<u>Mphatso za utsogoleri.</u>

Werengani Aefeso 4:11-13. Anthu ena analandira mphatso za utumiki kuchokera kwa Mulungu (vesi 7-10) kuti atumikre dera limene Mulungu anawapatsa. Atumwi, aneneri, alaliki amayendayenda mmipingo yosiyana siyana.

Atumwi amamangirira za uzimu monga Paulo, wotumidwa kukabyala mipingo yatsopano ndi kuthandiza mipingoyo kuti ikule ndi mphamvu.

Aneneri amabweretsa bvumbulutso lochokera kwa Mulungu kukonza zomwe anthu a Mulungu akuchita. Wonsewa ndi wokhuzidwa ndi kumangirira ndi kugwirizanitsa thupi la Khristu (mpingo).

Alaliki amayenda nalalikira uthenga wabwino kubweretsa anthu kwa Khristu ndi kuwaphunzitsa achite moyenera monga kunayenera ndi ena onse.
Mu nthawi ya chipangano chatsopano, munali atsogoleri monga tatchulawa. Kunalibe likulu la mpingo limene limalumikizana ndi mipingo yayingóno kuti ilimbikitsidwe ndi kudalira.

Tsopano tiyenera kuona atsogoleri m onga akulu ndi atumiki.

Akulu a mpingo.

Awa amatchedwa “oyangánira” ngakhale nthawi zina amatchedwanso “mabishopu” zosiyana kwa ndi tanthauzo la bishopu m’tsiku la lero lino.Akulu a mpingo ayenera kukhala ozindikira ndi okhazikika amene angathe kuphunzitsa ena.
Ngakhale atumwi ndiwo amawasankha, koma Mulungu ndiye amagwira ntchito yosankhayo (Machitidwe 20:28). Ntchitoyo ndi yoweta nkhosa za Mulungu (1 Petro 5:2).

Izi zikutanthauza kuti:

1. **Kudyetsa**. Sikungopereka chakudya kokha (kuphunzitsa mawu a Mulungu) komanso kuwatsogolera iwo ku msipu wobiliwira (Masalmo 23:2) kumene angaphunzire kuzidyetsa wokha kuchokera ku mawu Mulungu. Monga mwana wongobadwa kumene m’banja la Mulungu, muyenera kudyetsedwa chakudya choyenera. Makanda amafuna mkaka osati chakudya cholimba chotafuna (1 Petro 2:2).
2. **Kusamalira.** Monga Dotolo asamalira wodwala. M’gulu lililonse muli nkhosa zomwe sizamphamvu mu uzimu (1 Atesalonika 5:14). Akulu amadzipereka kuti nkhosa zichire ndiponso zikhale za mphamvu mu uzimu. Tiyenera kumvetsetsa zobvuta zawo kuti tithe kuwathandiza bwino.
3. **Umateteza.** Nkhosa zosatetedzedwa zimabedwa ndi akuba kapena nyama zolutsa mosabvuta. Paulo akuuza akulu a ku Efeso, dziyangánireni nokha ndi gulu lonse la nkhosa la Mulungu. (Machitidwe 20:28-31).Akulu ayenera kukhala tcheru pa gulu la nkhosa chifukwa ndi amene adzayankha kwa m’busa wamkulu Yesu(1 Petro 5:3-4).
4. **Kutsogolera.** Baibulo limaphunzitsa kuti m’busa amatsogolera nkhosa (Yohane 10:4) ndipo mibulu imene imabalalitsa nkhosa. Tikamati mtsogoleri ayenera kutsogolera, zimatanthauza kuti ayenera kupereka chitsanzo kuti otsatira atsatire (1 Petro 5:3).Amayenda patsogolo pa nkhosa osati kumbuyo kwa nkhosa kuzisonyeza nkhosa njira yabwino yoti ziyendemo.
5. **Kulamulira**. Nkhosa kuti zikhale ndi mbusa, ziyenera kukhala pansi pa ndodo ya m’busa (Ezekieli 20:37). Kukhala pansi pa ulamuliro wa m’busayo. Ngati nkhosa

sizikuzipereka, mbusa sangathe kuzitsogolera. Choncho mpatseni mwayi m'busa wanu pa moyo wanu kuti akuthandizeni inu kukhala mu uzimu. Si ulamuliro wa nkhanza, koma wa chikondi kuti inu mukhale wa mphamvu ndi wokonzedwa.

Atumiki.

Atumiki ndi gulu losankhidwa kuthandiza akulu a mpingo potumikira mpingo m'madera ena monga mwa mphatso zawo. Nthawi zambiri atumiki amakhala amuna (1 Timoteo 3:2) koma atumiki akazi amakhalaponso (Aroma 16:1; 1 Timoteo 3:11).
Ena salamulira kapena kupereka maganizo pa zokambirana, koma ngati akutumikira bwino akhoza kumakwedzedwa kutenga maudindo ena (1 Timoteo 3:13).

Kumvera akulu anu.

Mmene tingawamverere iwo ndi chimodzi modzi mmene tingamumvere Mulungu amene anawasankha. Tikulamulidwa mmawu kuti;

1. Lemekezani iwo koposa mwa chikondi chifukwa cha ntchito yao. Khalani mu mtendere wa inu nokha. (1 Atesalonika 5:12-13) Ayenera kugwira ntchito ndi mphamvu (vesi 12).

2. Mverani atsogoleri anu ndikuwagonjera ..(Ahebri 13:17). Kumvera, kuchita ndi kugonjera ndi kudzichepetsa. Mutha kumvera ndi kugonjera pa maganizo oipa. Yesu anamvera atate (Masalmo 40:8). Koma Yudasi anagonja kwa ndi maganizo oipa (Luka 22:48). Nthawi zina mutha kusamvera koma ndi maganizo abwino, koma izi zimachitika ngati pokha pokha mwapezana ndi mtsogoleri amene afuna kuti mumvere iye mmalo momvera Mulungu ngati mmene zinachitikira ndi atumwi (Machitidwe 5:29).

3. Khalani omvera ndi okhulupirika……Ngati mwachita zoyamba ziwiri, ichinso chikhoza kutsatira. Simungathe kutsutsa komanso kungúngúza, kapena kumvera ena amene achita ichi (Yakobo 4:11; 5;9). Ngati muli ndi bvuto ndi chinthu chilli chonse mkulu wa mpingo wanena kapena kuchita, iwo amayembekedzera kuti mupita ndi kuchinena chinthucho mosaopa.

Lowezani

Mverani atsogoleri anu, nimuwagonjere pakuti alindira moyo wanu, monga akuwerengera kuti akachite ndi chimwemwe, osati mwa chisoni (Ahebri 13:17).

Ntchito ya kunyumba.

1. Werengani za abusa onyenga pa Ezekieli 34:1-6 ndipo lembani zinthu zisanu ndi zitatu zimene iwo achita?(vesi 3-4), ndi ziwiri zomwe ndi zolakwika (vesi 2-4b).

2. Werengani zinthu zisanu zimene akulu a mpingo amachita, ndipo lembani maganizo anu pa mfundo iliyonse mmene inu mufunira kuti machitidwe awo akhale abwino.

Chiyambi cha phunziro 11.

KUTENGAPO MBALI.

Mpingo sunakhazikitsidwe kuti ukhale chionetsero kwa anthu, ndipo anthu otengapo mbali pa mpingopo mkukhala ochepa, amene aziyimba nyimbo pa tchalitchipo ndi kumanena Ameni pa mapeto pa mapemmphero. Amakhala ndi anthu amene ali a nsembe.

Taphunzira kale kuti chipangano chatsopano chimanena kuti Khristu ndi mutu wa Eklesia ndipo mpingo ndi thipi lake. Cholinga cha thupi lako ndi kuchita zomwe mutu wako ukuganiza, koma izi zimatheka pamene gawo lililonse la thupi lako likugwira ntchito yake bwino ndi kuchita zomwe mutu wako walamulira. Izi zili chimodzi modzi mu thupi la Khristu. Ndinu tsopano gawo la thupi la Khristu ndi cholinga muchite ngakhale kuti cholingacho simukuchidziwa kwenikweni.

Mu phunziro limeneli muphunzira kuti pali za uzimu zomwe muchite komanso zakuthupi ndi machitidwe amene mugwiritse ntchito, ku ulemelero wa Mulungu komanso kumtumikira ndi kudalitsa abale ndi alongo. Moyo wa kutumikira ndiwo kukwaniritsa cholinga cha moyo.

PHUNZIRO11.

KUTENGAPO MBALI .

Werengani: Aroma 12:3-13.

<u>Ntchito yopambana</u>.

Palibe ziwalo zopanda ntchito mthupi la Khristu. Inu munasankhidwa mthupi limenelo ndi cholinga (kumbukirani phunziro 3). Sikuti mungopita ku mwamba kokha ayi, komanso kuti muntumikire Iye pa dziko pano (1 Atesalonika 1:9).

<u>Kupeza malo anu.</u>

Ana amasewera masewera otchedwa ‘kufanizira’ ;amatsutsana za mdani akhale mtsogoleri. Nanga wina aliyense amatenga mbali yanji mu seweroli? Mu mpingo Mulungu anasankhira aliyense choyenera kuchita molingana ndi mphatso yake ndi umunthu wake. Ukakhala mu uzimu, zimayamba kubvuluka, ngati inu simudziwa, mtsogoleri wanu adzakudziwitsani.Pakali pano chimene mukuchita, chitani ndi mtima wonse (Mlaliki 9:10).

Kuphunzira kutumikira.

Chofunikira kwambiri si zimene timachita koma mmene timachita. Cholinga ndi chimene chimatilimbikitsa, koma kukhumba kutumikira anzathu ndiko kutumikira Khristu. Ndi zoona Mulungu akufuna ife tisangalale ndi kukwaniritsidwa komnso kutengapo mbali pa chisangalalochi kuti chikhale chopambana.

Wina wake ananena, ndinayang'ana pa mwana wa nkhosa wa Mulungu ndipo nkhunda ya mtendere ina ulukira moyo wanga. Ndinayang'ana pa nkhunda ya mtendere ndipo inathawa.

Mu phunziro 7, tinaona mphatso za mzimu kuti sizinaperekedwe kwa ife kuti zitipatse phindu ife koma kuti zitithandize ife kutumikira thupi la Khristu. Yesu ananena kuti "kutumikira ena ndi njira yokhayo angakwezedwe mu ufumu wa kumwamba, ndi kuti Khristu sanabwere kuzatumikiridwa koma kuzakutumikirani"(Mateyu 20:25-28).

Kutumikira kumaonetsa chikondi chimene sichitumikira potsata phindu lake (1 Akorinto 13:5),koma phindi la anthu ena (Afilipi 2:4). Mzimu woyera ndi wokonzeka kukudzadza ndi chikondi chotero (Aroma 5:5).

Ndiwe wansembe.

Mchipangano chakale, ansembe amakhala anthu osankhidwa mwapadera ndi Mulungu kuti atumikire anthu chifukwa chakuti antuwo paokha sakadatha kupereka nsembe. Okhulupirira mwa Khristu, sipafinikanso kuti pakhale wa nsembe pakati pa ife ndi mulungu monga zinali kucitikira ndi a Isiraeli. Koma ife tonse ndife ansembe (Chibvumlutso 1:6). Ndipo tili nawo malowedwe athu kwa Atate, mwa mzimu umodzi (Aefeso 2:18). Pokhala ansembe, sindiye kuti ndife atsogoleri, koma zimatipatsa mwayi wogwira ntchito za uzimu (monga kuyamika, kupembedza ndi kutimikira Mulungu (1Petro 1:25).

Kupereka nsembe za uzimu.

Usaganize pa iwe wekha kuti sindingathe kuchita ichi. Wayambapo kale kuchita koma iwe sukudziwa. Nthwi ili yonse imene ukupemphera kapena kuthokoza Mulungu pa iwe wekha, ukuchita monga wa nsembe ndipo ukupereka nsembe zako. Yamba kuchita pamodzi ndi banja lako, ndipo uona kuti sipadzakhalanso chobvuta pokhalira pamodzi ndi anthu ena. Pali zinthu zochepa zimene zizakondweretse anzanu pamene azakumvani inu kwa nthawi yoyamba.

Mudzalimbikitsidwa ndi kuyamba kutumikira pogawana nawo, kuchitira umboni, kupemphera, kupempherera ena, ndi kupereka matamando kapena kuchita mphatso ya mzimu ina iliyonse (1 Akorinto 14:26).
Pamene mukukula, mzimu woyera adzakuphunzitsani mmene mungatumikirire pansi pa ulamuliro wa mtsogoreli wanu.

Ntchito yochitika.

“Ngati ndi kutumikira, mloleni atumikire”(Aroma 12:7). Izi zikuphatikiza zochitika komanso kupezeka mu mmisonkhano. Ngati chikondi cha Mulungu chilli mu mtima mwanu, muli ndi mwayi wambiri kukwaniritsa zofuna za ena monga kuthandiza anthu, kusita, kuphika, kuchapa, kulima, kuwaza nkhuni ndi kuthandiza ena osowa.

Ena amadziwa zinthu zoti ena sangathe kuchita monga kumangirira mapaipi a madzi, amagetsi, kukonza mipando, kongoletsa, kusoka ndi zina zotero. Muzikhala ndi chimwemwe ndi kukondweretsedwa pochita zimenezi kwa ena mchikondi. Pakuchita izi, mudzakhala mukutumikira Khristu.

Lowezani.

Indetu Indetu ndinena ndi inu, chifukwa mwachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale wang’ono awa munachitira ine (Masalmo 25:40).

Ntchito ya kunyumba.

1. Werenganinso Aroma 12 mavesi 6-8 ndi 13. Pali njira 8 kapena 9 mmene tingatumikirire thupi la Khristu. Lembani mu kope lanu magawo awiri
   (a) Zochitika mmisonkhano
   (b) Zochitika kunja kwa msonkhano.

2. Lembani mndandanda mmene mukuganizira kuti mungatumikire ena. Sikuti mutengere pa zomwe mwalemba mmagawo awiri ena aja iyayi. Pempherani kwa Mulungu kuti akupatseni mtima wa chikondi kuti pakakhala chosowa, inu mutumikire podziwa kuti mukutumikira Khristu.

Chiyambi cha phunziro 12.

NKHANI ZA NDALAMA.

Ndithu ndalama ndi zofunika. Monga zili zofunika kwa inu, ndi zofunikanso kwambi kwa Mulungu. Ndi chifukwa chache chake baibulo likunenapo pa nkhani ya ndalama.
Palibe cholakwika ndi ndalama. Ndi zofunika kwambiri koma ikusokoneza anthu ambiri chifukwa amafuna zochuluka ndipo amagwiritsa ntchito njira yoipa.

Pa dziko munthu wa ndalama amalemekezedwa koposa kuti ndi munthu wanzeru, pamene wosauka amanyozedwa. Ngakhale sizili chomwechi mu ufumu wa kumwamba.

Maganizo anu pa ndalama ndi mmene mumaigwiritsira ntchito, zitha kuoneka ngati mayesero a khalidwe lanu.

Pamene Khristu anatenga inu kwa Iye, anakuchotsaninso ku zinthu zonse zimene muli nazo. Simungathe kuzipereka kwa thunthu kwa Iye osapereka zinthu zanu komanso ndalama zanu. Izi zikutanthauza kuti mulibe china chilli chonse, koma zonse zilipo kuti zigwiritsidwe ntchito kwa Mulungu.

Tsiku lina adzaimba mlandu anthu onse akugwiritsa ntchito chuma njira yolakwika. Phunziro ili, likuthandizani inu kukhala woyang'anira wabwino wa chuma cha Mulungu, kuti mudzakhale wowerengera wabwino pamene mudzafunsidwa.

PHUNZIRO 12.

NKHANI ZA NDALAMA

Werengani: 1 Timoteo 6:3 10.

<u>Ndalama ikhoza kukhala yoopsa.</u>

Baibulo limanena kuti ndalama njofunikira kwambiri mu ufumu wa Mulungu (Luka 16:9) komanso chikondi cha pa ndalama ndi muzu zoipa zonse (1 Timoteo 6:10). Ndalamatoyutu siyoyipa koma magwiritsidwe ntchito a ndalamayo ndiye woipa. Njira zotithandiza ife.

1. <u>Musaikondwtsertse.</u>
Musatengeke ndi kufuna kulemera mwachangu zomwe zikusokoneza dziko (1 Timoteo 6:6-10). Akutichenjeza zotsatira zake pamene tikhumba chuma. Tiphunzire kukhala okwaniritsidwa ndi zimene Mulungu watipatsa.

2. <u>Ndalama isakhale Mulungu wanu.</u>
Simungathe kutumikira Mulungu komanso ndalama. (Mateyu 6:24).Chili chonse chomwe mwaika mmalo mwa Mulungu ndi fano. Ena panopa anachoka pa maso pa Mulungu chifukwa anaika chuma kukhala chopambana kuposa osadziwa kuti chumacho chikuchokera kwa Mulungu (Hagai 2:8-9).

3. <u>Musankundike chuma</u>
Anthu amadzikundikundikira chuma ku dziko lapansi, kuti atetezedwe koma chimacho chimakhala chikusakazika (Mateyu 6:19). Musakundike chuma chosadziwika (1 Timoteo 6:17).Tiyenera kuika chuma chathu kumwamba mu ufumu wa Mulungu. Zimenezi sizingatiletse ife kukwaniritsa zofunika pa banja lathu(1 Timoteo 5:8).

4. Musalowe mu ngongole

Akhristu amene amakonda kungongola ndalama kwa anthu, amakhala akapolo a iye wowangongzayo komanso amanyozetsa chithunzithunzi cha ufumu wa kumwamba.

Ngongole yomwe taloledwa kukhala nayo ndiyo kukondana wina ndi mzake (Aroma 13:8). Nyumba zongongoza ndalama sizoti ukangongoleko ayi. Usalore kunyengereredwa kutenga ngongole poti umangire nyumba. Koma upewe izi. Magulu wokongoza, mabanki ndi ena otero asatinyengerere.

Ndalama zako ndi za Mulungu.

Monga mkhristu pamodzi ndi onse amene uli nawo achokera kwa Mulungu. Ndalama yako ili ngati talente imene Mulungu watipatsa (Mateyu 25:14). Mbuye wako amakupatsa iwe ndalama, amakupatsanso ufulu wogwiritsa ntchito chumacho koma ndi chake (Hagai 2:8). Akukuyetsani kuti aone ngati ndinu wokhulupirika (1 Akorinto 4:2) monga manijala wosamala kapena woononga (Luka 16:1)Tsiku lina tizafunsidwa za mmene tagwiritsira ntchito chuma chimenechi.

Kuphunzira kupereka.

Mulungu ndiye wopereka wamkulu ndipo palibe amene angamupose Mulungu kupereka (Yohane 3:16). Ndipo inu munaitanidwa kuti muchite chimodzi modzi monga Mulungu anachitira. Mukamapereka sikuti mukumnyengerera Mulungu, koma kuti mukudziwa kuti ndi mmene Mulungu amafunira. Ena ali ndi mphatso za kupereka (Aroma 12:8) osati chifukwa ali ndi chuma koma chifukwa ali ndi chikhulupiriro. Kulandira bwino alendo ndi kuwasamalira ndi chofunikiranso kwambiri pa kupereka (1 Petro 4:9). Kodi mungaperekw bwanji?

1. **Mwa ufulu ndi mwansangala (mokondwera 2 Akorinto 9:7).**
   Sizitanthauza kuti mupereke china chilli chonse koma perekani mokondweretsa Mulungu.

2. **Molingana ndi mmene wapezera (1 Akorinto 16:2).**
   Kumwamba kumaona mmene taperekera komanso zomwe tatsala nazo (Marko 12:41-44).

3. **Mwa dongosolo ndi mwa pemphero.**
   Osati modandaula kapena mokakamiza pomaliza ndi kutsaliratu opanda kanthu (1 Akorinto 16:2).

4. **Mwa nseri.**
   Musazionetsere mmene inu muperekera koma mwa dongosolo (Mateyu 6:1-4).

Kufesa ndi Kukolola.

Umu ndi mmene malemba amalinganizira za kupereka (2 Akoronto 9:6-11).Mbewu ili yonse imene ufesa, umayembekedzera kukolola mochuluka.Kuti munthu ukolole mochuluka, uyeneranso kufesa mochuluka (vesi 6) ndipo mochuluka momwemo

muzakololanso madalitso a uzimu osati chuma chokha (vesi 10). Mulungu akukulonjezani inu (Luka 6:38).

Chakhumi ndi Zopereka za ufulu.

Chakhumi ndi kupereka gawo limodzi la magawo khumi pa zomwe mwapeza kuchokera kwa Mulungu. Zopereka ndi mphatso zoonjedzera. Umatha kupereka mmene ukufunira ndi chifukwa chake zimatchedwa zopereka za ufulu
Mmatchalitchi, chopereka ndi chothandizira nacho abusa athu ndi ena amene amagwra nawo ntchito yotumikira pamene chopereka chimathandizira pa mpingo monga maulendo ndi zina ku ntchito ya Mulungu.
Pamene munthu akulephera kupereka chakhumi chotumikira nacho atumiki ake a Mulungu, amakhala akulanda zache za Mulungu (Malaki 3:8-10).

Lowezani

Patsani ndipo kudzapatsidwa kwa inu muyeso wabwino, wotsendereka, wokhuchumuka, wosefukira; anthu adzakupatsani mmanja mwanu ndi muyeso womwewo muyesera nawo inu (Luka 6:38).

Ntchito ya kunyumba.

1. Miyambo 3:9a, ikufotokoza maperekedwe athu kwa Mulungu. Lembani ndipo mumuuze Mulungu kuti ndi mmene mufunira kaperekedwe kanu.
2. Werengani 2 Akorinto 8:1-7. Tikuuzidwa mmene aku Makedonia anaperekera kuthandiza amene ali wosowa. Lembani mmene :-

   a) Paulo adafotokozera mu kubvomereza kwawo (vesi 9).
   b) Mmene chuma chao chinalili (vesi).
   c) Mmene Paulo anafotokozera kupereka kwawo (vesi 2).

   Werengani gawo la chakhumi chanu kuchokera ku zimene mudalandira pa mwezi kaya ndi pa chaka ndipo muike pa dera chakhumi cha Mulungu. Musadikire mukadzayamba kulandira malipiro a pa mwezi; mukhoza kuyamba pamene muli pa sukulu ndi ndalama imene mwapatsidwa kuti mukadyere. Patulanipo gawo limodzi la khumi. Mulungu adzatsegula mazenera kumwamba ndipo muyeseni ati Yehova……..

Chiyambi cha phunziro 13.

UFUMU ULI MKUDZA.

Pamene tikutseka gawo limeneli la kubwera pamodzi, tiyeni tione mozama pa ntchito yokhuza dziko lonse lapansi. “Ufumu wa Mulungu” Yesu ananena za mpingo molunjika kawiri kokha, koma nthawi zambiri anafotokoza za “ufumu wa kumwamba;” Kodi ufumu nchiyani? Kodi ndi wosiyana ndi mpingo? Nanga Yesu amatanthauzanji pamene amatiuza ife kuti tipemphere ufumu wa nu udze?

Kupeza mayankho a mafunso amenewa, pakufunika kuonjedzra nzeru zanu kuposa mmene mukudziwira popeza ndinu mmodzi wa gulu la mpingo wa pa dziko lonse lapansi umene uli pafupi kugonjetsa monga mmene Mulungu analonjezera.

Inu ndinu gawo la ufumuwo, ndipo ulemelero wake tsiku lina udzadza dziko lonse lapansi monga mmene madzi amazazira mnyanja.
Ichi chikulimbikitseni inu kutenga mbali pa kubwera kwa ufumu wa Khristu mmene inu mumakhalira ndi mmene inu muchitira umboni.

PHUNZIRO 13.

UFUMU ULI KUDZA.

Werengani: Mateyu 28 :16-20.

<u>Kumvetsa za Ufumu.</u>

Mmawu a Mulungu “ufumu” siutanthauza dera limene limalamulidwa munthu ngati mfumu ayi. Ufumu wa Mulungu ndi ulamuliro wa Mulungu pa miyoyo ya onse monga inu amene munazipereka ku ulamuliro wake (Mateyu 7:21), ndiponso ku dziko lonse ndi ku zochitika zonse za padziko.

Amalamulira zimene anthu amachita kukwaniritsa cholinga chake padziko lapansi (Danieli 4:34-35).

Mpingo ndi ufumu umene umafananirako koma ufumu koma ufumuwu umalimbikitsa zinthu zimene Mulungu akuchita pamene mpingo umalimbikitsa anthu amene Mulungu akuwagwiritsa ntchito mu mpingomo.

Mmene ufumu umabwerera

Mwaona kuti kutembenuka kumabwera ndi kulapa ndi kusiya ntchito zakale kubwera pa ulamuliro wa Mulungu (phunziro 5). Mu njira imeneyi mwalowa mu ufumu wa Mulungu (Akolose 1:13).

Kubwera kwa ufumu wa Mulungu, zikutanthauza kupanga malamulo a Mulungu agwire ntchito mmitima ya anthu ndi kuonetsa mphamvu pa moyo wawo kuti chifuniro cha Mulungu chikwaniritsidwe pansi pano(Mateyu 6:10).

Baibulo siliphunzitsa kuti dziko lizatembenuka (Chibvumbulutso 22:1) koma likulonjeza kuti mitundu izatembenukira kwa Mulungu ndipo izakhala cholowa chake kufikira malekezero a dziko (Masalmo 2:8).

Ngakhale panali ntsutso ndi mazunzo, mpingo mchipangano umayenda ndi mphamvu munthawiyo koteronso ndi dziko lonse lapansi nthawi yomaliza. Korona wa chipambano ndi kubwera kwa Khristu kudzaombola mpingo wake (phunziro 20). Nanga Mulungu adzaugwiritsa ntchito bwanji kuti ubweretse ufumu wake pa dziko?

Chikhalidwe cha ufumu.

Chikhulupiriro chanu chatsopano chabweretsa chikhalidwe chatsopano mmoyo wanu. Chikhalidwe chanu chasinthika ndipo chipitiliza kusinthikabe. Zochitika zina, zizolowezi, zilakolako ndi zokhumba zachotsedwa ndipo zatsopano zapangika pamene mwalola Khristu kulamulira.
Zolimbikitsa za ufumu wa Mulungu sizotsutsa koma zomumvera Iye. Timadziwika ndi zimene timachita osati chifukwa cha zimene sitichita. Pakuti ufumu wa Mulungu…….ndi chilungamo, mtendere ndi chimwemwe mwa mzimu woyera. Zomwe dziko lapansi silingakhale nazo koma likuzifuna kwambiri.

Zoona zake ndi zakuti makhalidwe amenewa ndi okondweretsa Mulungu ndi ovomerezedwa ndi anthu (Aroma 14:17-18). Iyi ndi njira yayikulu yolimbikitsira anthu ndipo inayambidwa ndi akhristu woyamba (Machitidwe 5:13). Komanso pali zina.

Kunena molimba mtima.

Kuchitira umboni ndi kuuza ena zimene Yesu Khristu wakuchitira mmoyo wako. Ndicho chimwemwe chako ndi mwayi wako ndi ntchito yako.Mzimu woyera anaperekedwa kutipatsa ife mphamvu ya kuchitra umboni (Machitidwe 1:8). Akhristu woyamba ngakhale analandira mzimu woyera, anapemphera kuti akhale ndi mphamvu zambiri ndipo anadzadzidwanso ndi mzimu chifukwa cha ntchito ya umboniyi (Machitidwe 4:29-31).

Uyenera kuchita chimodzi modzi. Siuyenera kuti udziwe zambiri kapena kuyankha mafunso ovuta, kungogawana ndi anzanu zimene Yesu anachita kwa inu. Munthu wosaona amene Yesu anamchiritsa, anabvomereza kuti sangathe kuyankha mafunso

amamufunsa iye koma chinthu chimodzi amachidziwa ndichakuti anali wosaona koma tsopano akuona (Yohane 9:25). Palibe yankho pamenepo.

Lowezani.

Pakuti ufumu wa Mulungu sukhala mchakudya ndi nchakumwa koma chilungamo ndi mtendere ndi chimwemwe mwa mzimu woyera (Aroma 14:17).

Ntchito ya kunyumba.

1. Kodi chikhalidwe cha moyo wako chasintha chifukwa chokhala mkhristu? Lembani mkope lanu.

    (a) Zimene mukudziwa kuti Mulungu wakusinthani mmachitidwe anu, chilankhulidwe chanu, zilakolako, ubale ndi kagwiritsidwe ntchito ka ndalama komanso malonda anu ndi zina.
    (b) Zimene mukufunabe kuti Mulungu asinthe. Pempherani kwa Mulungu kuti asinthe chilichonse chimodzimodzi.
2. Kuchitira umboni kwanu kukuyenda bwanji?
    (a) Nanga mwachitira kale umboni abale, abwenzi omwe mumagwira nawo ntchito ndi ena, funsani Mulungu kuti akuonetsereni zomwe muyenera kuchita. Mulungu akhoza kufuna kuti mulankhule nawo; ayitaneni ku msonkhano kapena apatseni kabuku kuti akawerenge. Ngati pali ena amene ndi koyamba, lembani zoti Mulungu achite nawo.
    (b) Ngati simunawachitire umboni abale ndi abwenzi anu, konzani mmene mungayambire. Pemphani Mulungu akuonetseni amene mungayambe naye ndi kulimbikisidwa. Koyamba zimabvuta koma kenako sizibvutanso.
    (c) Kaya muli pa A kapena pa B . Pemphani Mulungu kuti akudzodzeninso ndi mzimu wake ndi kupanga inu a mphamvu.

GAWO LACHITATU

KUKULA MWA MULUNGU.

PHUNZIRO 14-20

Mlimi anazindikira kuti imodzi mwa mbewu zake yayamba kufota. Sinali kukondwa, pomwe zina zinali kukondwa. Anayidzula mu mphika naona kuti mitsitsi yake inali itadyeka ndi tidzilombo. Anapha tizilomboto ndipo mbewuyo inayambaso kukondwa ndikukula bwino.

Monga mbewu ipeza zofunika zonse munthaka, inuso mupeza moyo wanu mwa Mulungu. Ngati zina sizili bwino ndi moyo wanu wauzimu, simungathe kukula bwino. Gawo limeneli likhudzana kwambiri ndi moyo wanu mwa Mulungu, kuonetsetsa kuti palibe choletsa inu kudalitsika ndi Mulungu wanu, pokhala mchiyanjano ndi Mulungu wanu.

Zomera zomwe timaziona zili kusangalala chifukwa mitsitsi yake ili bwino,ndipo ndiyobisika bwino. Pali zambiri mmoyo wachikhristu zomwe ndi zokoma ngati musamalira bwino chikhristu chanu. Mugawo lotsilizali, muphunzira mmene mungasungire moyo wanu wauzimu kuti ukhale wamphavu ndiwokula bwino kuti usafote.

CHIYAMBI CHAPHUNZILO 14

CHIKUMBUTIMA CHABWINO

Beru lachidziwitso lidalira panyumba pa mkulu wina wochita malonda, pakati pausiku. Apolisi anafika, koma sanapeze munthu chifukwa, linangolira lokha chifukwa cha vuto lamagetsi.

Chikumbutima chilli ngati beru lomwe limatidziwisa kuti china chake chalakwika mmoyo wanthu wa uzimu. Aliyense ali ndi chikumbutima chosiyana ndi zake chomwe chimabwera ndi unthenga wosiyanaso. Nthawizina beru, silila monga mmene kuyenera. Nthawi zinal imakhala vuto loti siliyenera kulila.
Kodi chikumbutima ndi chani?Nanga chimagwila ntchito bwanji?Chifukwa chiyani chikumbumtima chanu chimakusowesani mtendere pa zinthu zimene poyamba sizinali bvuto kwa inu musali mkristu? Phunziro lino likupatsani mayankho. Chofunika kwambiri ndi choti phunziroli likufokoza bwino za chikumbumtima chabwino ndi mungachipezere.

PHUNZIRO 14

CHIKUMBUMTIMA CHENICHENI.

Werengani: Aroma 2:12-16

<u>Chikumbumtima nchiyani?</u>

Ndichotumphuka mkati chimene chimatipangitsa ife kuganiza bwino pa kupanga chinthu chabwino kapena choipa. Ndi liwu la mkati limene lichita umboni kwa inu, kukutsutsani pamene inu mwalakwa kapena kukutetezani kuti musalakwe (Aroma 2:15).
Ngati musunga bwino chikumbumtima chimenechi, chimapatsa nzeru zoletsa inu pa zoipa. Titha kunena kuti tili ndi chikumbumtima chabwino kapena chenicheni (1 Timoteo 1:5).
Ngati muchinyozetsa, ndiye kuti muli ndi chikumbumtima choipa (Ahebri 10:22). Munthu wina aliyense ngakhale wosazindikira, amakhala ndi chikumbumtima.

<u>Kodi nchodalilika?</u>

Mtsogoleri wa anthu opha nyama za ku tchire (Mlenje), akhoza kukhala opanda chifundo pofuna kupha munthu wa mtundu lina, komu ndikumakhuzika kuti aphe nyani

chifukwa anamva kuti nyani ndi myama yopatulika ndipo aliyense wopha nyani angaone zosaona.

Zimene zimalowa mmaganizo anu kuti izi ndi zoipa kapena zabwino zimatsimikizira mmene chikumbumtima chanu chimagwirira ntchito. Ubongo wanu uli makina a komputa. Ngati muigwiritsa bwino ntchito idzakupatsani uthenga wabwino.

Pamene mwadziwa Mulungu ndi kuwerenga mawu ake, muzukhala ndi kuganiza kwabwino kosangalatsa Mulungu kosiyana ndi nthawi imene inu munali musanadziwe Mulungu.

Kodi ndi chiyani chimachitika potembenuka mtima?

Pamene uthenga ulalikidwa kwa inu, mzimu woyera umagwiritsa ntchito chikumbumtima chanu kukutsutsani inu. Ndi ntchito ya mzimu kuti inu mukafike potsutsika mdziko lochimwa (Yohane 16:8).

Pamene uthenga wa choonadi unalowa mmaganizo anu, unawalitsa chikumbumtima chanu ndi kuzindikira tchimo, zinapangitsa inu kubwera kwa Khristu.

Pamene mugwiritsa ntchito choonadi cha chifuniro cha Mulungu, chikumbumtima chanu chimawala. Izi sizikutanthauza mumakhala mu uchimo nthawi ndi nthawi, koma inu mumakhazikika pa choonadi cha Mulungu nthawi zonse.
Paulo analankhula ndi wokhulupirira amene anali ndi chikumbumtima chofooka kuti amangotsutsika pen pali ponse (1 Akorinto 8:7-8). Chikumbumtima cheni cheni chimachotsa bvuto lotere. Kumbukirani za beru lolira chifukwa cha akuba linalira popanda wakuba chifukwa linali ndi bvuto la magetsi.

Ndi chokoma kwambiri kudzadzidwa ndi nzeru ya chifuniro cha Mulungu (Akolose 1:9).

Kodi chikumbumtima choona ndi chofunika?

Ndi chofunika kwambiri. Chipulumutso chathu chimatimasula ife ku uchimo (Aroma 8:1). Koma ngati chikumbumtima chako ndi choipa, umakhala nsutsano mkati mwako. Izi zimaononga:-

1. **Chiyanjano chako ndi Mulungu**

Sungathe kusangalala pamaso pa Mulungu. Mwana amasowa mtendere pa maso pa makolo ake ngati wachita cholakwa.

2. **Chikhulupiriro chako**

Chikumbumtima ndi chikhulupiriro cha mphamvu siziyendera limodzi. Mukungolapa tchimo lanu, chikhulupiriro cha mphamvu chimakhazikika.

3. **Moyo wanu wa pemphero**

Munthu anabwera kwa khristu mpemphero ndipo mzimu woyera anamkumbutsa kuti; ali mnyamata anaba thumba la misomali pa wopala matabwa. Akamati apemphere, amaona thumba la misomali lija. Ndi pokhapo anabwerera ndi kukabwezera thumba la misomali lija ndipo atatero anatha kupemphera bwino.

4. **Chilakolako chanu pa mawu a Mulungu.**

Chikumbumtima cholakwika chimamuchotsa munthu pa mawu a Mulungu. Ngakhale awerenge mawu sapeza malo okhazikika mmoyo wake. Mawu a Mulungu ndiwo chakudya cha moyo wa uzimu.

5**. Umboni wanu.**

Utha kufuna kuti ulalikire kapena uchitire umboni za Yesu, koma satana amakunena kuti ndiwe wabodza sungathe kuchitira umboni za Ambuye Yesu. Ngati ukhazikitsa nthawi yoti ambuye azikulankhula koma osaigwiritsa ntchito. Nthawiyo ikafika, umakhala utagona. Uli chimodzimodzi munthu wosamvera ndipo kulankhula kwa Mulungu kumasiya kumveka kwa iwe.

Mungasunge bwanji chikumbumtima choona?

Pali magawo anayi:

(a). **Lapa msanga tchimo lako**

Lapa pamene wazindikira kuti wachimwa(1 Yohane 1:9). Monga mmene Ambuye Yesu anaphunzitsira “mutikhululukire mangawa athu”(Mateyu 6:12). Tizakhala opanda machimo tikamatero. Tsopano pamene mwalapa;

(b). **Khulupirirani lonjezo la kuyeretsedwa**

Mulungu ndi wokhulupirika ndi wolungama kutichotsera chosalungama chilli chonse ndi kutitsuka m’mwazi wache (1 Yohane 1:9). Chikumbumtima chathu chimatsukidwa ndi mwazi wa Yesu pamene tichitira umboni (Ahebri 9:14). Mukatero.

(c). **Mverani chikumbumtima chanu**

Chitani chilungamo ndipo siyani kuchita tchimo. Kuulula kokha sikukwanira koma kuleka kuchita tchimolo.

(d). **Pitirizani kuyenda mkuwala**

Khalani womasuka kwa Mulungu ndipo mvetserani zimene mzimu woyera anena ndi inu mkati mwanu ndipo konzekani kumvera ndi kuchita nthawi yomweyo. Lowezani

Mmenemonso ndidziyetsera ndekha ndikhale nacho nthawi zonse chikumbumtima chosanditsutsa cha kwa Mulungu ndi kwa anthu(Machitidwe 24:16) Mawu a Paulo mtumwi.

Ntchito ya kunyumba.

1. Wonetsetsani kuti muli ndi chikumbumtima choona. Ngati palibe chokubvutani musataye nthawi ndi kufufuza chinthu chomwe mu mtima mwanu mulibe. Yamikani Mulungu chifukwa cha madalitso okhala mkuwala ndi Mulungu. Ngati chikumbumtima chanu sichili bwino koma bvutolo silikupezeka, pempherani monga anapemphera Davide pa Masalmo 139:23-24. Ndipo pamene Mulungu ayankha, tengani magawo anayi ali pamwambawa agwire ntchito.

2. Mukuthandiza munthu amene waulula machimo ake kwa Mulungu koma sakupeza mtendere kuti wakhumudwa. Lembani mu kope lanu zomwe mungachite pomuthandizanzanuyi . Werengani 1 Yohane 1:9 ikuthandizani.